

PITANI, MUKAWAUZE



Kuchitira umboni, ndipo mlongo wamng'ono kumbuyo uko, ine ndikuganiza izo zikuifotokoza nyimbo imeneyo:

Oh, chikondi cha Mulungu, ndi cholemera
bwanji ndi choyera!

Nchosayezeka ndi champhamvu bwanji!

Ndi tsiku lotani limenelo kwa ife! Tiyeni basi mwakachetechete, ndi mitu yathu yoweramitsidwa tsopano, tiyimbe imeneyo kwa Ambuye tisanapemphere. Basi, Teddy, ngati iwe ungate, kutipatsa ife poyambira pang'ono. Ndipo tiyeni ife tingoimba iyo kuti . . . ndi mitu yathu yoweramitsidwa, maso athu otsekedwa, basi tisanapemphere.

Oh, chikondi cha Mulungu, ndi cholemera
bwanji ndi choyera!

Chosayezeka ndi champhamvu bwanji!

Chidzakhhalapo nthawizonse . . . [Malo opanda
kanthu pa tepi—Mkonzi].

² Ngati inki, madzi onse akanasanduka inki, ndi thambo lonse litapangidwa kukhala pepala, ndipo phesi lirilonse pa dziko lapansi cholemba, ndipo munthu aliyense kukhala mlembi, komabe izo sizingakhoze kufotokoza chikondi cha Mulungu kwa mtundu wakugwa wa Adamu. Ife tikukuthokozani Inu, Atate, chifukwa cha Magazi ofunika awo a Ambuye Yesu, ndi chifukwa cha mmawa wachikumbutso uja wa chiwukitsiro, ndi chifukwa cha chikondi Chanu chowombola chimene chatsanuliridwa mmitima mwathu lero, ndi Mzimu Woyera. Kutibweretsa ife mu chiyanjano ndi Iye, Waumulungu Uyo, Mlengi. Kutibweretsa ife mu ubale, pa dziko lapansi, umene sunayambe waposedwapo. Palibe loji, palibe lumbiro, sizingakhoze konse, kufaniziridwa nkome ndi ubale wa amuna ndi akazi obadwa mwatsopano. Ndipo idzakhala kwanthawizonse nyimbo ya ojera ndi angelo!

³ Ife tikupemphera lero kuti Inu mukadalitse zonse zimene ife tikuchita pakuyesera kufotokoza, kwathu—kuyamikira kwathu mmitima mwathu kwa Inu, chifukwa cha chimene Inu mwatichitira ife. Ndipo kudziwa kuti sikuti inali mitima ya ophunzira okha imene idakondweretsedwa mmawa umenewo, Maria ndi Maria wa Magadala, koma ifenso, ophunzira Anu lero, mitima yathu imakondweretsedwa ora limene ife tipeza kuti Iye sali wakufa, koma ali moyo. Mulole Iye akhalebe wamoyo mmitima mwathu, pakati pathu. Ife tikupempha mu Dzina la Yesu. Amen.

Sipangakhale aliyense amene angafotokoze za chiukitsiro!

⁴ Tsopano, mmawa wachiukitsiro uno, ndi nthawi yopambana kwambiri kuti zochitika zazing'ono zichitike mu tchalitchi

tsopano, ndizo, amayi kudalitsitsa ana awo. Icho ndi chinachake chatsopano, china chawonjezeredwa ku nyumba zawo. Mdalitso wina watsopano wabwera kwa iwo. Ndipo iwo akufuna, mobwezera, apereke izo kwa Mulungu.

⁵ Ndipo kenako pambuyo pa—uthenga wa mmawa, ife tikhala ndi pemphero kwa odwala, kuti inu mukaukitsidwe kuchoka ku matenda anu, kukalowa mu thanzi latsopano. Kenako mwamsanga zikangotha zimenezo, kwa iwo amene sanabatizidwe, ife tidzakhala ndi chiwukitsiro cha zimenezo; kudzaikidwa mmadzi, kuti tidzawuke ku moyo watsopano. Zimenezo palimodzi ndi chiukitsiro mmawa uno, chiukitsiro! Mitima yathu yapangidwa kusangalala ndi kupepuka, pamene ife tikuimba nyimbo ndi kumvetsera ku maumboni a ena, za mmawa wodabwitsa wa chiukitsiro uwu. Ndipo ife tikuyang'ana kunjani ndipo ife tikuwona Mulungu akusangalala nazo zimenezo, mitengo ikuwukitsidwa.

⁶ Nthawi ina kale, uko ku Kentucky, Bambo Wood ndi ine timasaka agologolo, ndipo ife tinapita ku malo a bambo wina. Munthu ameneyo akhoza kukhala kuti ali pano pakadali pano, kwa zonse zimene ine ndikuzidziwa. Ndipo iye amayenera kukhala wachikunja. Ndipo M'bale Wood anamufunsa iye, anati, “Kodi ine ndingasakeko agologolo ku malo anuwa?”

Iye anati, “Inde, Wood, iwe ukhoza kukasaka agologolo. Kazipita.”

Iye anati, “Chabwino, ine ndabwera ndi abusa anga.”

⁷ Ndipo iye anati, “Wood, iwe sukutanthauza kundiuza ine kuti iwe wafika potsika kwambiri kuti iwe ukumachita kumayenda ndi mlaliki nthawi zonse!”

⁸ Ndipo chotero iye anandiitanira ine kumeneko kuti—kuti akandidziwitse ine. Ndipo munthuyo anali atanena kuti iye anali ngati munthu wovuta. Iye anauzidwa ndi ena, kuti, koma iye samatha kuwona chirichonse chomupangitsa iye kuti akhulupirire.

⁹ Ndipo pamenepo panali mtengo wa apulo unali pamenepo umene ine ndinali nditathyolamo apulo. Munali mu Ogasiti. Ndipo ine ndinati kwa njondayo, ine ndinati, “Mtengo uwu uli ndi zaka zingati?”

¹⁰ Ndipo iye anati, “Zaka sarte zinazake,” chinachake kapena chimzake. Iye anali ataubzala iwo.

¹¹ Ndipo ine ndinati, “Inu mwakhala mukudya maapulo kuyambira pamene unayamba kubereka?”

“Inde, bwana.”

¹² Ine ndinati, “Chimachitika ndi chiyani kwa mtengo umenewo? Ngati inu mungayang'ane pa iwo, pano ndi mu Ogasiti, kwakhala kuli nyengo yotentha chiyambireni; koma tsopano masamba akugwa mu mtengo umenewo, ndipo

utomoni ukuchoka mu nthambi, kupita pansi ku mizu. Ngati iwo ungakhale pameneo kudutsa dzinjali, mtengowo sungakhaleenso moyo; koma iwo umapita pansi kukalowa mu dothi, kuti ukadzibise wokha ku mphepo yozizira. Ngati iwo angakhale pamwamba apa, iwo ungafe, iwo sungathe kubereka ma apulo aponso. Koma iwo umapita pansi kukadzibisa wokha ku mizu, kuti udzabwererense chaka chotsatira, kuti udzakubweretsereni inu ma apulo ena kuchokera kwinkakwe, ndi masamba ena.”

¹³ Ndipo ine ndinati, “Tsopano, bwana, ine—ine ndikukupemphani inu mundiuze ine ndi Luntha lanji limene limapangitsa utomoni umenewo kuti uchoke mu mtengo isanafike nyengo yozizira iliyonse, ndikupita pansi ku mizu kukabisala? Ngati inu mungandiuze ine chimene chimachita zimenezo, ndikuzifotokoza izo kwa ine, chimene chimachita izo, ndiye ine ndikulolani inu kuti muike dzanja lanu pa Mulungu.” Ine ndinati, “Inu muike madzi pa mtengo ndipo muwone ngati iwo ungachite zimenezo, muwone ngati kusintha kwa nyengo kungachite zimenezo. Pali Nzeru ina yaikulu imene imayendetsa utomoni umenewo kupita pansi ku muzu wa mtengo, ndipo kenako nkuwubweretsa iwo kenanso ndi moyo watsopano. Ameneyo ndi Mulungu.”

¹⁴ Ndipo iye anati, “Ine sindinapitepo ku tchalitchi mochuluka kwambiri.” Iye anati, “Koma panali mlaliki wina anabwera kuno ku Acton, nthawi ina, ndipo anamuza mzimayi wina, amene ankakhala pa phiri, yemwe mchemwali wake anali ku msonkhano usiku umenewo, ndipo anamuza iye kuti iye anali kupempherera mchemwali amene anali ndi khansa.” Ndipo anati, “Mkazi wanga ndi ine timapita kumeneko kukamuthandizira iye.” Ndipo anati, “Iye anali moyipa kwambiri, ndi khansa ya mmimba, kufikira kuti iwo amachita kumusuntha pa bedi limodzi ndi zofunda, ndi zina zotero. Mlongo wake anabweretsanso mpango,” anati “bamboyo atamuza iye za momwe analiri ndi zonse, anati ‘ukayike mpangowo pa iye.’” Ndipo anati, “Iye ali bwino lero.”

¹⁵ “Ndipo izo zikungowonetsera,” ine ndinati, “Luntha lomwelo limene limauza utomoni umenewo mu mtengo, chaka ndi chaka, inu muli chipenyere, kuti upite pansi ku mizu kuti ukabisale, linali Luntha lomwelo limene linandiiza ine kuti mzimayi ameneyo akachiritsidwa pamene iye akaika ka...” Ine ndinati, “Zimenezo si chi—chinsinsi kwambiri. Inu muli ndi mlaliki wabwino kwambiri waima patsogolo pa bwalo lanu, mtengowo, amene amakuuzani inu chaka ndi chaka.”

¹⁶ Ngati ife titamayang’ana pozungulira, ife tizimuwona Mulungu paliponse. Iye ali mu mtengo uliwonse, tsamba lililonse la udzu. Palibe chirichonse chingapange izo koma Mulungu. Ife tikhoza kupanga chinachake chowoneka ngati izo; koma osati moyo umenewo, iwo ndi Mulungu.

17 Tsopano, katsamba kakang'ono ka udzu kawonjezedwa ku makomo ena pano, ndipo ife tikufuna kuwadalitsitsa ana aang'ono awa kwa Ambuye. Teddy, ife tiri ndi nyimbo yaing'ono apa ife timaimba, *Abweretseni Iwo Umo*, iwe ungaimbe imeneyo pamene amayi amene akufuna kuti ana awo adalitsidwe, ndi abambo, azibweretsa ana awo aang'onowo kuno pa guwa.

18 Ndipo ife tiri ndi maluwa ambiri aang'ono a Isitara pano pa guwa mmawa uno, sichoncho ife? Mai, mai! Ine ndikulingalira pali a Mary aang'ono, a Ruth, a Rebekah, a James aang'ono, Paul, ndi John, onse ali pamenepa, maluwa aang'ono a Isitara kwa kam'badwo kena.

19 Zonsezo ndi zabwino, pamenepo. Ine ndikukhulupirira M'bale Beeler akufuna kutenga chithunzi ichi cha uyu—munthu wamng'ono uyu waima apa, ndi—ndi mdzukululu wa M'bale Wood, Mlongo Wood pamenepo. Ndipo ena akubwera tsopano ndi ana awo. Bwerani patsogolopa, abwenzi. Ndizo zonse zabwino. M'bale Neville.

20 Chopambana ndi chilumikizano cha chikwati choyera, icho chinadzozedweratu ndi Mulungu. Ndipo kudzera chikwati choyera chimabweretsa ana aang'ono okonedwa awa.

21 Inu muyenera mudiuze ine dzina lake apa tsopano. Brenda Sue. Iwe ukuwoneka mosiyana kwambiri, mwana, kusiyanana ndi momwe ine ndinakuwonera iwe poyamba. Chabwino, apa pali Brenda Sue Wood wamng'ono, ndithudi chuma chofunika chaching'ono kwa mitima ya ife tonse, ndipo makamaka kwa mayi wamng'ono uyu ndi bambo.

22 Ndipo mu nthawi za Baibulo. Anthu ambiri amawakonkha ana aang'ono awa; koma ife timayesetsa kutsatira kachitidwe ka Baibulo mwapafupi momwe ife tingathere. Ife sitinawonepo pamene iwo anayamba akonkhedwapo, mu Baibulo, koma iwo amabweretsedwa kwa Ambuye Yesu ndipo Iye amawadalitsa iwo. Ndipo ife timawayangata iwo, monga antchito Ake, ndi kuwatukulira iwo kwa Iye.

23 Ine ndikukhulupirira kuti inu mukudziwa momwe agogo ake aliri wonyadira, inu mukudziwa. Chotero tiyeni tiweramitse mitu yathu mphindi chabe.

24 Ambuye Yesu, Mwana wa Mulungu, Yemwe anaperekedwa chifukwa cha zolakwa zathu. Ndipo icho ndi chinthu chofunika kwambiri kuwona aang'ono awa akubweretsedwa kwa Inu, pokumbukira zimene zinachitika zaka zambiri zapitazo, pamene amayi ndi abambo anawabweretsa ana awo kwa Inu. Ife tikuyangata pamaso Panu, lero, mmikono ya chikhulupiriro, Brenda Sue Wood wamng'ono, yemwe watumizidwa ku banja la M'bale wathu David ndi mkazi wake wofunika. Atate Mulungu, mudalitseni mwana uyu.

25 Iwo akuvomereza chikhulupiriro chawo mwa Inu, pamene iwo akupereka mphukira zawo ku chilumikizano chawo. Ndipo

ife tikupemphera kuti Inu mukawadalitse iwo. Ndipo mulole mitima yawo itenthetesdwe ndi Mzimu Woyera, akakhale moyo waumulungu chomwecho, miyoyo yodzipatula, kuti mwana uyu akaleredwe mu nyumba ya Chikhristu, kukuzidwa mu kuphunzitsidwa za Mulungu, ndi kukhala moyo wautali, wokondwa pano pa dziko lapansi, ndi kukutumikirani Inu masiku onse a moyo wake. Ndipo mu Ulemelero, pamene mabanja adzakasonkhane kumeneko, mulole Brenda Sue wamng'ono ndi bambo ake ndi amayi, ndi anthu awo onse, adzakasonkhane kuzungulira mpando wachifumu wa Mulungu, wowomboledwa mwa chisomo cha Khristu, kwa amene ife tikumukwezera kwa Iye tsopano.

²⁶ Mlongo wanga wamng'ono, ine tsopano ndikukupereka iwe kwa Ambuye Yesu Khristu, ku moyo womutumikira Iye, mu Dzina la Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu. Amen.

²⁷ Mulungu akudalitse iwe, Marilyn, David, chisangalalo chochuluka ndi kupambana. Mulole wamng'onoyu akhale moyo ku Ufumu wa Mulungu.

²⁸ Tsopano, apa pali mnyamata wabwino, kumwetulira kwakululu kopambana pa nkhope yake. Dzina lake? [Amayi akuyankha. Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi].

Sharon Rose . . . [Amayi akuti, “Sharon Daulton.”—Mkonzi.] Daulton. Daulton. Kodi uyu ndi mwana wa M'bale Ed? Chabwino, mwinamwake, pafupifupi zaka twente thuu zapitazo, Mulungu anamchotsa mmikono yanga Sharon Rose wamng'ono, amene ali Kumwamba, lero. Ndipo tsopano, kuti timupereke kwa Iye, ndi Sharon Rose Daulton wamng'ono. Ife tikumudziwa M'bale Ed ndi Mlongo Daulton, pano, monga abwenzi athu ofunika. Ndi mwana wokondedwa bwanji!

Atate athu Akumwamba, ife tikumubweretsa kwa Inu Sharon Rose wamng'ono uyu. Pokumbukira Ambuye Yesu wamkulu, Yemwe anadzaima pa dziko lapansi, ndipo iwo anamubweretsera Iye atsikana aang'ono monga chonchi, Ine ndikumupempherera mwana uyu, Ambuye. Mulole iye akhale moyo ndikukhala wamphamvu ndi wathanzi. Mulole iye akhale moyo kwa ulemelero wa Mulungu. Mudalitse bambo ake ndi amayi. Mulole iye aleredwe mu uphungu wa Mulungu. Iwo akuvomereza chikhulupiro chawo mwa Inu pamene iwo akupereka mwana wawo kwa Inu. Tsopano ife tikupereka kwa Inu, Sharon Rose Daulton wamng'ono, kuti Inu mudalitse moyo wake, Ambuye. Ine ndikumupereka iye kuchokera mmanja mwa amayi ake ndi abambo, kupita kwa Inu, Ambuye Wanga, ndi Mpulumutsi, Yesu Khristu, kwa ulemelero Wake. Amen.

Mulungu akudalitseni inu, mlongo, ndi inu, m'bale.

Oh, mai! Mnyamata wamng'ono, wodwala. Vuto lake ndi chiyani? [Amayi akuti, “Mutu wake ukukula kwambiri. . .”

Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi]. . . chinachake chosiyana. Ine ndikumukhulupirira Iye.

Ambuye, Mulungu, ine ndikunyamulira kwa Inu Mason wamng'ono. Ine ndikupemphera, Ambuye Yesu, kuti Inu mumutenge mwana uyu amene ine ndamunyamula mmanja anga, kuti ndimudalitsire iye kwa Inu. Ine ndikutemberera kusautsa uku pa iye. Mu Dzina la Yesu Khristu, mulole Mason wamng'ono ayikidwe mmanja Anu, Ambuye, ndipo mulole kusautsako kumusiye iye. Mulole mwanayu akhale moyo kwa ulemu ndi ulemelero wa Mulungu. Makolo akuwonetsera chikhulupiriro chawo pamene iwo akumubweretsa iye. Inu mumuchiritse mwanayo ndikumupanga iye kukhala wabwino bwino. Mulole iye akhale moyo kwa ulemelero wa Mulungu, kuti adzakutumikireni Inu. Ambuye Mulungu, ine ndikumpereka kwa Inu Mason wamng'ono, mu Dzina la Yesu Khristu, kwa moyo wake ndi machiritso ake. Amen.

[Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi]. Mungokhulupirira ndi mtima wanu wonse.

Oh, mtsikana wamng'ono, apanso? Chabwino, ziri bwino. Bwera kuno, kanthu kakang'ono. Udzaima pomwe apa. Dzina lako ndi. . . [Abambo akuti, “Sumner.”—Mkonzi]. Sumner. M'bale ndi Mlongo Sumner. Ine ndikukhulupirira ndinu ochokera ku Georgia, sichoncho inu? Ine ndimaganiza kuti ndinakumbukira pemphero. Pali anthu ambiri kumusi kumeneko. Uyu ndi. . . [“Latrelle.”] Latrelle. [“Dwight.”] Dwight. [“David.”] Ndi David. Inu mwamva dzina lawo. Mulole Mulungu alembe maina awo pa Bukhu la Moyo la Mwanawankhosa.

Atate athu Akumwamba, ife tikuwabweretsa okonedwa aang'ono awa kwa Inu mmawa uno, pamene ine ndaika dzanja langa pa zingongo zazing'ono pa mutu pawo, tsitsi laling'ono lofewa la anyamata awa. O Ambuye, adalitseni iwo. Makolo awo awonetsera chikondi chawo ndi chikhulupiriro chawo mwa Inu powapereka ana awo. Ndipo ife tikuwapereka iwo kwa Inu, Ambuye, monga iwo atengedwa kuchokera mmanja a makolo, kuti adzaima pano pa guwa lino mmawa uno, kudzapatulira miyoyo kwa Mulungu. Adalitseni iwo, Atate. Ife tikupemphera kuti Inu muwalole iwo akhale moyo kuti adzakhale osangalala, masiku onse a moyo wawo, Moyo Wamuyaya mu dziko limene likubwera. Mulole iwo akaleredwe mu uphungu wa Mulungu, mu nyumba ya Chikristu.

Tsopano, mwa kutuma kwa Yesu Khristu, anapereka chitsanzo kwa atumiki Ake, kuti iwo adzatsatire monga momwe Iye anachitira, Ine ndikuwapereka iwo kwa Inu, mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

[Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi].

Kutali kumusi mu dera la kuwala kwa dzuwa la Georgia, mwana uyu wabweretsedwa pano ndi abambo ake achikondi ndi amayi ake, kuti adzadalitsidwire kwa Inu pa mmawa wa chikumbutso uno. Iye ndi chikho cha chisomo Chanu m’banja lawo. Ine ndikupemphera kuti Inu mumudalitse Renee wamng’ono, amayi ake ndi bambo. Ndipo iwo akuwonetsera chikhulupiro chawo mwa Inu, pomubweretsa mwanayu, akufuna madalitso Anu pa iye. Ndipo mulole iye akhale moyo ndi kukhala Mkhristu wamphamvu, wosangalala, masiku onse a moyo wake; ndi kukhala ndi Moyo Wamuyaya mu masiku amene akubwerawa, mu dziko limene likubwera. Perekani izi, Atate. Monga Inu munanyamulira tinthu tating’ono tokoma totere, monga ana awa mmawa uno, mmanja Anu momwe, mabanja awonetsera chikhulupiro chawo mwa Inu, powabweretsa iwo kwa antchito Anu. Ndipo ife tikudalitisa Renee wamng’ono ndi kumupereka iye kwa Inu; kuchokera mmanja a makolo ake, kupita kwa Inu. Mu Dzina la Yesu Khristu, Inu mumudalitse iye. Amen.

Akudalitsemi inu, m’bale. Mulungu akudalitse iwe, Renee.

Tiyeni tingoimba ndime yaing’ono ya iyo.

Abweretseni iwo, abweretseni iwo,
Abweretseni iwo kuchokera ku minda ya
tchimo;
Abweretseni iwo, abweretseni iwo,
Abweretseni aang’onowo kwa Yesu.

²⁹ Oh, momwe ine ndikanakondera kuima pa mzere ndi kuyankhula zokhudza aliyense wa aang’ono amenewo, koma ine basi ndangokhala wochedwa kwambiri, mulimonse, ndipo anthu angoima. M’bale Wood anandiuzwa ine mmawa uno, anati nsana wake umangopweteka, chifukwa choimirira. Inu simukudziwa momwe ine ndimakuyamikirirani inu chifukwa choimirira ndi kudikirira! Ndipo ine ndingokhala wofulumira ndi uthenga, mmene ndingathere. Ndipo inu mumvetsera mwacheru kwenikweni.

³⁰ Ine sindinakhale ndi nthawi yokonzekera msonkhano wa mmawa uno, kapena uthenga uwu mmawa uno, mphindi chabe. Ine ndinatenga mutu ndi chinachake chimene chinali chosiyana.

³¹ Ndipo Isitara yathayi ine ndinalalikira pa phunziro: “*Pokhala Moyo*, Iye anandikonda ine. *Pakufa*, Iye anandipulumutsa ine. *Poikidwa Mmanda*, Iye anatengera machimo anga kutali. *Powuka*, Iye anandilungamitsa kwaulere kwanthawizonse. Tsiku lina Iye *Adzabwera*, oh, tsiku laulemerero!”

Ndiyeno mmawa uno ife tinalalikira pa phunziro: *Ine ndikudziwa*.

³² Ndipo tsopano, ngati Ambuye alola, ine ndikufuna kuti ndiwerenge kuchokera mu mutu wa Marko Woyera. Ndipo inu mupemphere ndi ine tsopano.

³³ Ndipo mwamsanga ukangotha uwu kukhala msonkhano wa machiritso. Ndipo kenako ukatha msonkhano wamachiritso kukhala msonkhano wa ubatizo. Ndipo kenako misonkhano ikhalapo usikuuno pa hafu pasiti seveni.

³⁴ Tsopano Marko 16.

Ndipo pamene sabata inatha, Maria Magdalena, . . . Maria amake a Yesu, ndi Salome, anali atabweretsa zonunkhiritsa zokoma, kuti iwo akakhoze kubwera ndi kudzamudzoza iye.

. . . molawilira kwambiri mmawa tsiku loyamba la sabata, iwo anabwera ku manda pakutuluka kwa dzuwa.

Ndipo iwo ananena pakati pa iwoeni, Ndani adzatigudubuzire ife mwala kuchoka pa khomo la manda?

Ndipo pamene iwo anayang'ana, iwo anawona kuti mwalawo unali utachotsedwapo: pakuti iwo unali waukulu.

Ndipo polowa mmanda, anawona bambo wachichepere atakhala mbali yakumanja, atavekedwa chovala chachitali choyera; ndipo iwo anachita mantha.

Ndipo iwo anati kwa iwo . . . Ndipo iye anati kwa iwo, Musachite mantha: Inu mukufuna Yesu wa ku Nazareti, amene anapachikidwa: iye wauka; iye sali kuno: taonani malo amene iwo anamugoneka iye.

Koma mupite pa njira yanu, ndipo mukawauze ophunzira ake ndi Petro kuti iye watsogola akupita ku Galileya: kumeneko inu mukamuwona iye, monga iye ananenera kwa inu.

Ndipo iwo anatuluka mofulumira, ndipo anathamanga kuchoka mmanda; pakuti iwo ananjenjemera ndipo anadabwa: mpaka kuti sanakambe kalikonse kwa munthu aliyense; pakuti iwo anali ndi mantha.

Tsopano pamene Yesu anawuka molawilira tsiku loyamba la sabata, iye anawonekera koyamba kwa Maria Magdalena, mwa iye amene anatulutsamo ziwanda seveni.

Ndipo iye anapita kukawauza iwo amene anali ndi iye, pamene iye . . . pamene iwo anabuula ndi kulira.

³⁵ Inu mwaona, iwo anali pa mulu wa phulusa, nawonso.

Ndipo iwo, pamene iwo anamva kuti iye anali moyo, ndipo anali atawonedwa ndi iye, sanakhulupirire.

36 *Momwe Mawu a Mulungu aliri a chinsinsi!*

Zitatha zimenezo iye anawonekera kwa . . . mmawonekedwe ena kwa awiri a iwo, pamene iwo amayenda, ndipo anapita mu dziko.

Ndipo pamene . . . ndipo anapita ndipo anakawauza izo kwa otsalira: ngakhale sanakhulupirire iwo.

Zitatha izo iye anawonekera kwa khumi ndi mmodzi pamene anakhala pa chakudya, ndipo anawadzudzula iwo ndi ku- . . . ndi—ndi kusakhulupirira ndi kuuma kwa mtima, chifukwa iwo sanawakhulupirire iwo amene anamuwona iye atauka.

Ndipo iye anati kwa iwo, Pitani inu ku dziko lonse, . . . kalalikireni uthenga kwa chorengedwa chirichonse.

Iye amene akhulupirira nabatizidwa adzapulumutsidwa; . . . iye amene sakhulupirira adzawonongedwa.

Ndipo zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira; Mu dzina langa iwo azidza tulutsa ziwanda; iwo adzayankhula ndi malirime atsopano;

Iwo adzatola njoka; . . . ngati iwo adzamwa kalikonse kakupha, iko sikadzawapweteka iwo; iwo adzaika manja pa odwala . . . iwo adzachira.

Chotero pamenepo Ambuye atatha kuyankhula nawo iwo, analandiridwa kumwamba, ndipo anadzakhala pa dzanja lamanja la Mulungu.

Ndipo iwo anapita, ndipo anakalalikira ponseponse, Ambuye akuchita ndi iwo, ndi kutsimikizira mawu ndi zizindikiro zikutsatirapo. Amen.

37 *Ine ndikufuna kutenga mutu kuchokera pa mawu awiri: Pitani, Mukawauze.*

38 *Inu mukudziwa, sizimakhala zabwino kwambiri kupita ngati iwe ulibe chinachake choti ukawauze. Ine ndikuganiza ndiro limene lakhala liri vuto lalikulu lero. Ife timapita kukawauza, ife timapita koma sitimakhala ndi choti tikawauze, wopanda chirichonse cha phindu chirichonse, wopanda kanthu koti kangakawathandize anthu.*

39 *Koma ngati ife tingatsatire malangizo monga ophunzira awa amene analandira kutuma, ifenso tidzakhala ndi kutuma komweko, “Pitani, mukawauze ophunzira Anga kuti ine ndauka kwa akufa.” Pitani, mukawauze zimenezo!*

40 *Kenako Iye akuti, “Pitani, mukalalikire iwo, ndipo mukawonetsere zizindikiro izi kuti Ine ndiri wamoyo ndachoka kwa akufa.” Uthenga bwanji! “Pitani, mukawauze, ndipo pitani,*

mukawawonetse ophunzira Anga zinthu izi zimene mwaziwona, kuti Ine sindiri wakufa, koma ndauka kwa akufa.”

⁴¹ Mu Uthenga wa mmawa uja mmawawu, ife tinapeza kuti mmodzi aliyense wa ife timakhala ndi milu ya phulusa yaing’ono ya mavuto ndi mayesero pamene ife timakhala titamatikapo, nthawizina, kudikirira chitonthozo. Ife tinapeza kuti mbadwa yaikulu Yobu anali ndi masomphenya, chifukwa iwo anali asanakhalepo ndi Isitara apobe, koma iye anawona zaka foro sauzande kutali mmawa uwu. Iye anawona zaka foro sauzande kutali, Isitara, ndipo anafuula, mu kupsyinjika kwake, “Ine ndikudziwa Muomboli wanga ali moyo! Masiku otsiriza, Iye adzaima pa dziko lapansi. Ngakhale mphutsi za khungu zingawononge thupi ili, komabe mu mnofu wanga ine ndidzamuwona Mulungu.”

⁴² Tsopano, itatha Isitara, ife tikupeza kuti Mulungu anampatsa munthu kutuma, “Pitani, mukawauze! Ndipo ngati inu mukawauze, *izi* zidzakutsatirani inu. Pitani ndipo mukawauze!”

⁴³ Tsopano, izo sizimakhala zabwino, monga ine ndinanenera, kuti upite, kuti upite, pokhapokha iwe utakhala ndi chinachake choti ukanene. Ndipo ngati iwe uli ndi uthenga wolakwika kuti ukanene, ndiye izo sizimachita ubwino uliwonse. Iwe umayenera ukanene chimene chiri chinsinsi.

⁴⁴ Nthawi ina kale ine ndinali kuwerenga mu bukhu, za mnyamata wamng’ono amene anali... analowa mu mpikisano. Ndipo mu mpikisano umenewu iye ankayenera kudzipangira yekha dzina lotchuka. Mnyamata wamng’ono aliyense amene akanatha kusunga mawu achinsinsi mmutu mwake kufikira iye atafika pa malo enaake, ndipo iye amatha kuwatchula mawu a chinsinsi amenewa, ndipo wapachipata amamulola iye kuti adutse. Zimenezo zinali kuti ayese Kaganizidwe ka mwanayo. Ndipo pamene iye anafika pa malowo, kuyankhula mawu a chinsinsi amene anaperekedwa kwa iye, chipata chikanatseguka ndipo iye akanadzapambana ulemu waukulu.

⁴⁵ Mnyamata mmodzi wamng’ono, pokhala anali wopepuka mapazi kwambiri, ndipo amadziwa bwino lomwe ndi mwabwino kuti iye akanatha kuwapitirira anyamata ena onsewo mu mpikisano, kapena iye ankaganiza kuti akanakhoza. Iye amayeserera tsiku ndi tsiku, kumathamanga. Momwe iye ankapopera mapapo ake aang’ono, thupi lake atalichepetsa, kuti iye asamatope pamene iye akuthamanga. Ndipo iye anayeserera momwe iye angayambire ndi mapazi ake, ndi kuwutsogoza mutu wake patsogolo pa anyamata ena onsewo. Ndi momwe iye ankayenera kupumira pa nthawi ya kuthamanga kwake, ndi cholinga choti aziwugwira mpweya umene umabwera ku thupi lake, kuti zimuthandize iye kupitirira kupopabe, kuti izo

zisakachedwetse mtima wake kwambiri. Iye anaziphunzira izo kuchokera pa ngodya iliyonse imene iye akanatha.

⁴⁶ Ndipo mmawa umene mpikisano unayambika, panali anyamata aang'ono oposa handiredi ndi fifite atafola, a usinkhu winawake. Mnyamata wamng'ono uyu anali wa usinkhu wabwino, pa msinkhu wake. Ndipo iye anakumbukira kuphunzira kwake konse. Ndipo iye anakonzeka. Iwo anafika pa mzere, ndikudzaika nkhope zawo zazing'ono motsamira chichingwe chimene chinali pamenepo, anakankhira mphuno zawo zazing'ono pa icho. Iye anali atawerenga malamulo onse a izo, kudzikonzekeretsa yekha.

⁴⁷ Ndiyeno pamene mfutiyo inadzawombera, ndipo chingwecho nkudzaduka, anyamata aang'onowo analumphira kutsogolo. Ndipo mnyamata wamng'ono uyu anali wathanzi kwambiri mpaka iye analumphira kutsogolo kwambiri kwa ena onsewo. Ndipo iye anapita akusesereka ndi liwiro lowopsya, wophunzitsidwa bwino, kufikira kuti iye amakhoza kupitirira mnyamata aliyense amene anali pa mpikisanowo. Ndipo iye anali pamenepo, oh, kwanthawi yaitali ndithu, mwinamwake miniti kapena kupitirira apo, asanafike pamalopo katswiri wa othamanga enawo.

⁴⁸ Koma, kuphunzira kwake konse kwathupi, iye anali ataiwala mawu achinsinsi. Iye anali ataiwala chinthu kumene chimene iye amayenera kuti adzanene, kuti iye adzalowe pa chipatacho. Ndipo anathamangira mmbuyo ndi mtsogolo, ndipo anaganiza za iwo, ndipo anasanthula mmalingaliro mwake. Iye anali atakomedwa kwambiri ndi zathupi, zochitika zakuthupi za thupi lake, kufikira kuti iye anaiwala chinthu chenichenicho. Akupitirira, kutsika mzere, anyamata ena amene samathamanga mwaliwiro kwambiri, anakumbukira mawu achinsinsiwo, ndipo anadzalowamo.

⁴⁹ Zirinso chimodzimidzi lero! Ife timakondweretsedwa kwambiri ndi kukamanga malo opatulika aakulu, ndi matchalitchi ndi zimango, ndi zina zotero, ndipo timakhala ndi chidwi kuti matchalitchi athu aziwoneka bwino, ndi zomanga zabwino ndi mipando yabwino yamtengo wapatali ndi malimba abwino. Azitumiki athu ophunzitsidwa bwino kuchokera ku...Iwo azikhala ndi Doctor DL., Ph.D., LL.D. madigiri, koma ife timaiwala chimene ife tikuthamangira. Ndiro limene liri vuto lake. "Pitani, mukawauze ophunzira anga kuti Ine ndawuka kwa akufa ndipo Ine ndikakumana nawo iwo ku Galileya." Ife tayiwala mawu otsegulira. Ife tatanganidwa kwambiri ndi zinthu zina, kumanga matchalitchi akulu akulu, tikumamanga zipembezozazikulu, mpaka kuti tikumaiwala mawu otsegulira.

⁵⁰ Miyoyo yambiri yapulumutsidwapo chifukwa chakukonzekera pa zochitika zimene zikubwera. Nthawi ina

kale, ine ndinauzidwa kuti ku Florida, munthu wowerenga nkhani, nthambi ya zanyengo, inatumiza nkhani kuti panali kubwera nkuntho waukulu. Ndipo munthu wina anali woweta nkukhu, ndipo iye anapita kwa oyandikana naye nyumba ndipo anakamuza iye kuti nkuntho umabwera. Iye sanalabadire, ndipo anati, “Zamkhutu!” Ndipo iye basi amapitirirabe. Iye sanalowetse nkukhu zake. Iye sanapite mosungiramo mwake. Iye sanapange madongosolo aliwonse. Ndipo woyandikana naye nyumba anapanga madongosolo. Koma zonse, za iye amene sanatenge chenjezo, nkukhu zake zonse zinaulutsidwa ndi kuphedwa, nyumba yake inagwa pansu, ziweto zake zinatayika, iye anatengedwera ku chipatala. Zonsezo chifukwa chakuti iye sanamvere chenjezo! Iye anadziwa uthenga unali utaperekedwa, koma iye analephera kumvera uthenga.

⁵¹ Umo ndi momwe zabwerera lero, ndi anthu athu ambiri, ndi mipingo yathu yambiri. Iye tikudziwa kuti Baibulo limaphunzitsa kuti Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Iye timadziwa kuti Baibulo limaphunzitsa, Yesu anati, mu Yohane Woyera 14:12, “Iye amene akhulupirira pa Ine, ngakhale, ntchito zimene ine ndizichita iye adzazichitanso; ntchito zazikulu zoposa izi iye adzazichita, chifukwa ine ndikupita kwa Atate.” Tsopano ife tachita chidwi ndi zinthu zina, osatenga chenjezo, osamvera. Iye tathamanga, koma osamvera ku Uthenga. Iye tapita, koma ife sitinadziwe choti tikawauze ife tikakafika kumeneko.

⁵² Masiku angapo apitawo pamene matchalitchi a dziko lino, pamene matchalitchi Achikhritsu anachititsidwa manyazi ndi chitonzo, pamene wantchito wolemekeza ndi wodziwika ndi woopa Mulungu, Billy Graham, anabweretsedwa maso ndi maso ndi Baibulo. Iye anali atathamanga, koma anali ataiwala Uthenga; pamene wa Chimuhamedi ameneyo anaima pamaso pake ndikumuuza iye, “Ngati awa ali Mawu a Mulungu, tiyeni tikuwoneni inu mukuwawonetsera Iwo.” Iye anali atathamanga bwino, zitsitsimutso zazikulu, zinthu zazikulu. Koma, pamene zinadzafika pamalopo, iye analibe Uthenga.

⁵³ “Ine ndauka kwa akufa. Ndine yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.” Kuthamanga mwathupi, matchalitchi abwino, mamembala ambiri, zipembedzo zazikulu, koma zimenezo sindicho chenichenicho. Taonani chimene chinadzatsatira, “Ndipo zizindikiro izi zidzawatsata iwo amene akhulupirira.” Pitani, koma sanadziwe choti akawauze.

⁵⁴ Mulungu sanamutumizepo munthu pokhapokha Iye atamupatsa iye chinachake choti akanene. Mulungu nthawizonse amatsimikizira Mawu Ake.

⁵⁵ Kupita, koma osakakhoza kukayankhula pamene iwe wafika kumeneko. Ziribe kanthu zitsitsimutso zanu ndi zazikulu bwanji, momwe tchalitchi chanu chiliri chachikulu, kapena

ndi mochuluka bwanji chipembedzo chanu chimaposera zinazo, ngati inu mulibe chinachake choti mukawauze iwo, inu muli ndi chiyaninso ngati si mulu wa anthu osonkhana pamodzi monga mphanga?

⁵⁶ Ife tiri ndi Uthenga woti tiliwuze dziko, “Yesu ali moyo! Iye sali wakufa!” Kumvera Uthenga!

⁵⁷ Mu fuko lalikulu lino limene ife tiri othokoza chifukwa cha ilo, la United States of America, mu chisokonezo chake chonse, mu zonyansa zake zonse, mfundo zake zonse zoipa, komabe ilo ndi fuko lalikulu pa dziko lapansi, ndipo pachiyambi, chifukwa ilo linali litaikidwa bwino. Ilo silinyamulepo Uthenga.

⁵⁸ Zaka zambiri zapitazo, pamene ilo linali pa ukhanda wake, nkhani ikubwera mmalingaliro anga, kuti aku Britain amayenera kutenga kayendetsedwe ka chuma ka fuko lino. Ndipo panali pali gulu la amuna amene anadzisonkhanitsa okha ndipo anali pa ntchito, akuyang’anira. Ndipo apo panali pataima kavalo atamangidwa, ndipo womukwera atakonzeka kuti amukwere miniti iliyonse. Chinthu choyambirira chimene iye anachipeza chinali chizindikiro chakuti ma British amabwera, ndipo iye anamukwera kavalo wake. Zikanamuchitira iye ubwino wanji kuti atulutse kavalo wake? Zikanachita ubwino wanji, kuti amenye kavaloyo ndi kuyesera kupanga njira yake kuchoka ku tchalitchi chimenecho kupita ku Boston? zikanachita ubwino wanji kwa iye ngati iye analibe uthenga woti akawauze anthu? Iwo akanadziwa bwanji kuti azikonzekeretse iwoeni?

⁵⁹ Paul Revere wathu wamakono wathamanga bwino, koma, iwo akungothamanga, palibepo Uthenga. Ora lafika, mavuto ayambika! Dziko liri pa mapeto! Mipingo yafika chiindeinde chake. Mafuko akumana ndi chiindeinde chake. Moyo wa munthu wakumana ndi chiindeinde chake. Sayansi yakumana ndi chiindeinde chake. Ife tachita chibungwe ndipo tapanga matchalitchi aakulu, tawapukuta azilaliki athu ndipo mwathupi tawaika iwo pamodzi, mwakuti iwo akudziwa momwe angagwiritsire ntchito ma verebu ndi adiverebu, ndi mamvekedwe awo ndi—ndi mawu awo onse, ndipo chirichonse chiri molondola basi mukuwerenga maganizo, kuti akawakhudze anthu. Koma zimenezo si zimene Yesu ananena!

⁶⁰ “Mu Dzina Langa iwo adzatulutsa ziwanda. Iwo adzayankhula ndi malirime atsopano. Ngati njoka yokupha ingawalume iwo, iyo siidzawapweteka iwo. Ngati iwo adzaika manja awo pa odwala, iwo adzachira.” Dziko likusowa mthenga ndi Uthenga, kuti likanene chinachake, ndi kudziwa kumene Uthengawo ukuchokerako ndi kwa Yemwe Iwo ukuchokerako.

⁶¹ Paul Revere, pamene iye anakwera pa kavalo wake, mwamuna wolimba, munthu amene ali mu mbiriyakale bola

ngati pali fuko loti lidzakhale ndi mbiriyakale yake. Iye anapanga kuyenda kumeneko kodziwika kuchokera pa masitepe a tchalitchi, ndi uthenga umene unamudzidzimutsa aliynese, kuchokera kwa wosaukitsitsa kupita kwa wolemera kwambiri, kuchoka kwa mlimi kupita kwa wazamalonda, “ma British akubwera!” Ndipo asilikali amtopola anadzikonzekeretsa okha kuti akaukire. Ndipo fuko lalikulu ili linapululumutsidwa.

⁶² Ngati cholowa cha Mulungu ichi, ngati anthu awa amene Mulungu anawafera, ngati Mpingo uwu umene unaitanidwa ndi Dzina Lake, ali woti udzapulumutsidwe, ife tikuyenera kukhala ndi mthenga ali ndi Uthenga wochokera pa Mpando wachifumu kuti akakumane ndi chitsutso cha tsiku lino. Pali Goliati, koma ndithudi Mulungu adzakhala ndi Davide penapake. Ife tikuyenera kufika pokumanizana. Ife tikuyenera kukhala ndi . . . Ife tikuyenera kukhala ndi Uthenga.

⁶³ Ife tikupita, koma tiribe chirichonse choti tikanene. Izo zikutsimikizira izo, pamene ife tifika pamalo amene fuko kapena anthu amene akukana Yesu Khristu kukhala Mwana wa Mulungu, ndipo nkuima pamaso pa azitumiki athu ovuta kwambiri a lero. Ndipo kenako mu mgwirizano wathu waukulu wa mpingo, kupeza Achikominisi ena sarte atanyamula mapepala kwa zaka twente kapena sarte, kuti iwo ndi mamembala a gulu la Chikominisi, mu mipingo yathu yangwirizano. Kodi ife tingachite chiyani? Izo zikuwonetsera kuti iwo athamanga opanda Uthenga; akugulitsa maufu oyamba kubadwa kumene a fukoli, akugulitsa mafulu oyamba kubadwa a nthawizonse a Mpingo.

⁶⁴ Izo zonse zafika pa chiwonetsero. Izo zafika pamalo akuti Mpingo waung’ono umene wakhulupirira Uthenga, ndipo ukuima ndi mapazi awiri onse, ndi maso awo atalunjika pa Mtanda, mu mtima mwawo chiwukitsiro cha Yesu Khristu, chikuyaka! Izo zafika pamalo akuti mafuko akuyenera kuti azizindikire Izo. Icho ndi chiwonetsero. Nzosadabwitsa kuti mipingo . . . Pamene Mgwirizano wa Mipingo, yalowereredwa kwambiri ndi Chikominisi, nzosadabwitsa iwo sangakhulupirire mu chauximu. Nzosadabwitsa iwo sangakhulupirire mu machiritso Auzimu; iwo alibe Uthenga uliwonse mu mtima mwawo, ziribe kanthu ndi molimba bwanji momwe iwo akuthamangira.

⁶⁵ Ngati Mzimu Woyera ubwera mu mtima wa munthu, iye adzakhulupirira kuti Yesu Khristu anauka kwa akufa, ndipo Iye ali moyo mwa iye, kuti achite, ndi kuti adzachite chifuniro chimene Iye anadzera kuti adzachite; chifuniro, chifuniro cha Mulungu kudzera mu moyo wa munthu.

⁶⁶ Koma, vuto, ife timathamanga, ife timapita opanda Uthenga. Ife timapita ndi fioloje. Ife timapita ndi mtundu wina wa kutanthauzira kwa Malemba kwa tchalitchi.

67 Ife tikuyenera kupita ndi chiukitsiro! “Pitani, mukawauze ophunzira Anga kuti Ine ndipanga mpingo watsopano”? Ayi, bwana! “Pitani, mukawauze ophunzira Anga kuti ine ndauka kwa akufa, monga ine ndinanenera kuti ine ndikanakhala.” Umenewo ndiwo Uthenga kwa Mpingo mmawa uno, kuti Yesu sali wakufa. Iye ali moyo, ndipo basi wamkulu ndi wamphamvu lero monga Iye wakhala akukhalira.

68 Ife takhala ndi mauthenga ochuluka a kuchenjeza, kuti tikonzeke, Paul Revere ndi amuna ena aakulu, ndi zinkhondo zazikulu ndi mikuntho, ndi zinthu.

69 Kenako, Mulungu anatomiza Uthenga wa chitonthozo, nayenso. Uwu unali Uthenga wa chitonthozo.

70 Nthawi ina kale, pamene iwo anali ndi ukapolo Kummwera, Mabunu atabweretsedwa kuchokera ku South Africa mbadwa, zimene ife timawatcha, lero, “munthu wachikuda.” Ndipo iwo anawabweretsa iwo kuno ndi kudzawagulitsa iwo kwa Achimereka Kummwera, kuti akawapange iwo kukhala akapolo.

71 Kuwukira kwakukulu kokhudza izi mu Africa lero, kuphedwa, ndi zina zotero, zikupitirirabe. Iwo akumenyera ufulu wawo. Iwo ali ndi ufulu woti amenyere iwo. Mulungu anampanga munthu; munthu anapanga akapolo. Izo sizinapangidwe kuti zizikhala chomwecho.

72 Zaka pang’ono zapitazo, ine ndinali mu coliseum, kapena mosungira zakale mwamukulu, kani. Ine ndinali kuyenda kuyenda, ndikuyang’ana zithunzi zosiyanasiyana ndi zinthu, chifukwa ine ndimayamikira zaluso. Ine ndikuganiza Mulungu amakhala mu zaluso. Ndipo ine ndinayenda mokwera, ndipo ine ndinazindikira panali bambo wachi Negro wachikulire, iye anali wokalamba kwenikweni, wakugwa mmapewa ake, atangokhala ndi ka mkombero kakang’ono ka tsitsi kumbuyo kwa mutu wake. Iye anali atavala chipewa chake. Ndipo iye amayenda yenda, ndipo chinachake mwakachitidwe *kameneko*, akuyang’ana pozungulira, ngati kuti iye amayang’anayang’ana kapena kufunafuna chinachake mosungira zakalemo. Ine ndinaima kumbuyo ndipo ndinamuyang’ana iye kwa kanthawi pang’ono.

73 Ndipo patapita kanthawi iye anabwera kukabokosi kakang’ono kenakake pamenepo. Ndipo iye anayang’ana mkati mwake, ndipo iye anadzidzimuka, ndipo maso ake anawala. Iye analumpha kuchoka pa kabokosiko kwa miniti, anachotsa chipewa chake chaching’ono, anachigwira icho mmanja mwake. Ndipo ine ndinkamuyang’ana iye. Ndipo pamene wokalamba woderapoyo anaweramitsa mutu wake, misonzi inayamba kutsikira mmasaya ake. Ndipo ine ndinamuyang’ana iye ndi chidwi, kwa kanthawi pang’ono.

74 Kenako ine ndinaganiza, “Ine ndifufuza kuti ndi chiyani chimene munthu wokalambayo amasangalala nacho kwambiri.”

Ine ndinayenda mozungulira mbali *iyi*, ndipo izo zinawoneka kwa ine ngati diresi inali mmenemo.

⁷⁵ Ndipo ine ndinayang'ana pa iye ataima pamenepo. Ndipo ine ndinapita pomwepo, ine ndinati, “Muli bwanji, malume?”

Ndipo iwo anati, “Muli bwanji, bwana.”

⁷⁶ Ndipo ine ndinati, “Ndine mtumiki. Ine ndimadabwitsidwa kukuwonani inu mukupemphera pa malo awa.” Ine ndinati, “Ine ndingakhulupirire kuti ndinu Mkristu.”

Iye anati, “Ndi choncho, bwana.”

Ndipo ine ndinati, “Ndi chiyani chomwe chakusangalatsani inu kwambiri?”

⁷⁷ Iye anati, “Bwerani kuno.” Ndipo ine ndinayenda ndi bambo wachikulireyo, cha pamenepo. Iye anati, “Inu mukuiwona diresi imeneyo?”

Ine ndinati, “Inde, bwana.”

Iye anati, “Inu mukuwona dontho limenero pamenepo?”

Ine ndinati, “Inde, bwana.”

Anati, “Ikani dzanja lanu pa mbali panga.”

Ine ndinati, “Ndi chiyani malo okhakhala amenewo?”

⁷⁸ Iye anati, “Lamba waukapolo anadutsa mozungulira pamenepo, tsiku lina. Ndipo *amenewo* ndi magazi a Abraham Lincoln.” Iye anati, “Magazi ake anachotsa lamba wa ukapolo pa ine.” Anati, “Kodi zimenezo sizingakusangalatse iwe, aponso?”

⁷⁹ Ine ndinaini pamenepo ndiri wozizwa. Ine ndinaganiza, “Ngati magazi a Abraham Lincoln angamusangalatse—angasangalatse kapolo, chifukwa chochotsa lamba waukapolo pa iye, Magazi a Yesu Khristu akuyenera kuchita chiyani kwa anthu ngati Rosella pano, amene anali kapolo wauchidakhwa; kwa ine, akufa, womvetsa chisoni?” Iye anachotsa lamba wa ukapolo wa tchimo mu mtima mwanga. Kodi zimenezo sizikuyenera kumusangalatsa munthu? Kodi izo sizikuyenera kumupanga iye kumverera mosiyana? Kodi izo sizikuyenera kumupanga iye kulemekeza pamene iye aganizira za zimenezo? Inu simungathe kuwuwona mtengo wopanda kuweramitsa mutu wanu, nkomwe, podziwa kuti Yesu anawombola moyo wanu pa Mtengo umenewo.

⁸⁰ Pamene ife tikupitirira, mphindi, ndi akapolo, ndi ganizo lathu. Pamenepo panali kulengeza, Kumasula kwa Chidziwitso, kumene kunasainidwa, ndipo akapolo anali oti adzakhala afulu pa tsiku linalake. Inu simukudziwa, oh, ngati inu simunakumanepo naye Khristu, inu simungadziwe chimene icho chinkatanthauza kwa akapolo amenewo. Pamene izo zinapita, uthenga pa dziko lonse, kuti, “Inu mudzakhala afulu pa tsiku lakuti-lakuti, masana. Inu mukhala afulu. Inu simumadzavalanso lamba wa ukapolo kenanso, ndiponso

inu simudzalandiranso zikwapu zina. Koma inu ndinu afulu, ndipo inu ndi mbadwa za United States wopambanayu. Inu simudzakhalanso kapolo, akadzadutsa masana a tsiku lakuti ndi lakuti mmawa.” Oh, ndi chiyembekezero chachikulu iwo anadikirira.

⁸¹ Ngati wochimwa atangokhoza kuwona zimenezo! Ngati wochimwa atangokhoza kumva Uthenga woona! Osati kujowina kwa mpingo, koma kulalikira kwa Uthenga, kuti inu mukhoze kumasuka ku tchimo, kuti inu mukhoze kumasuka ku nthenda yanu. “Pa nthawi yakuti-yakuti,” imeneyo ndi nthawi imene iwe umakhulupirira.

⁸² Inu mukudziwa, akapolo amenewo anali osangalala kwambiri pansi pa chiyembekezero chimenecho, akudikirira ora limene iwo akanadzakhala amfulu, kufikira, iwo amandiuza ine, kuti iwo onse anali atasonkhana pansi pa phiri, amayi ndi ana aang’ono, onse anasonkhana, ndi ena a okalamba. Ndipo iwo anakwera pamwamba pa phiri, cha pakati pa usiku. Iwo anali akudziwa kuti pamene tsiku liti liziyamba ndipo dzuwa likamatuluka, kuti iwo akanadzakhala afulu. Izo sizidzatengera theka la miniti imodzi kuti dzuwa lituluke kuchokera pamwamba pa phiri, koma ena a iwo anali pamwamba pa phiri, akuyang’ana yang’ana, akuyang’ana yang’ana. “Oh, dzuwa likamatuluka, ife tikhala afulu.” Ameneyo anali m-w-a-n-a . . . kapena, d-z-u-w-a.

⁸³ Koma pamene M-w-a-n-a adzatulukira limodzi la masiku awa! Ndipo pamene M-w-a-n-a anatulukira zaka naintini handiredi zina zapitazo, Iye anathyola lamba aliyense wa ukapolo, Iye anamasula kapolo aliyense kuti akhale mfulu, Iye anachiritsa nthenda iliyonse, Iye anapereka ufulu kwa iwo amene ali a msinga. Momwe ife tikuyenera kukwera ndikuyang’ana!

⁸⁴ Ndipo pamene dzuwa linadzasuzumira, koyamba, munthu amene anali pamwamba kwambiri, analiwona ilo, ndipo iye anafuulira pansi kwa munthu winayo, “Ife ndi afulu!” Ndipo munthu winayo anafuulira kwa munthu wapatali pansi pa phiri, “Ife ndi afulu!” Mpaka izo zinafika ku msasa, “Ife ndi afulu!” Pakuti, dzuwa linali likutuluka, iwo amadikirira, kudikirira, kudikirira ora limenero.

⁸⁵ Ndi mochuluka bwanji momwe ife tikuyenera kukhala odikirira, lero, kumudikirira M-w-a-n-a wa Mulungu. Ife ndi afulu kwa tchimo. Ife ndi afulu kwa maunyolo. Ife ndi afulu ku zizolowezi. Ife ndi afulu kukusuta, kumwa, zokongoletsa, chifukwa M-w-a-n-a wa Mulungu wauka kuchoka mmanda ndipo wadula msinga zonse. Kutsutsika konse kwatha! Ngongole yalipiridwa. Chilango chalipiridwa. Machimo achotsedwera kutali, ndipo ife ndi afulu. Oh, ife ndi afulu, anthunu! Ukapolo?

Ufulu, pamene Mwana wa Mulungu watulukira ndi machiritso mmapiko Ake!

⁸⁶ Tsikulina Iye adzauka kuchoka pa Mpandowachifumu, adzabwereranso pa dziko lapansi. Ndipo pamene ipo ife tidzakhala afulu ku zowawa zonse ndi mayesero onse, afulu ku zowawa zonse za thupi la chivundi ndi chirichonse chimene chimakhudzana ndi moyo wachivundi, kuti tikakhale ndi Iye kwanthawizonse. Ife tidzakhala afulu. “Pitani, mukawauze,” ndicho chinthu choyenera kuchita.

⁸⁷ Mu nthawi ya Baibulo, pamakhala chaka cha chisangalalo chinkabwera. Anthu amene ankagulitsidwa chifukwa cha ngongole zimene anali nazo, Iwo anali ndi ngongole ndipo sankatha kuilipira iyo, chotero iwo ankapita ndipo amakadzikulitsa okha kwa anthu, ngati akapolo. Ndipo iwo ankapita kukhala akapolo awo, kapolo wawo, moyo wawo wonse. Koma, kawirikawiri, pamabwera tsiku la chisomo, chimene chinkadziwika ngati chaka chachisangalalo. Ndipo pamene chaka chachisangalalo chifika, ndipo pamene pamapita wansembe ndipo amakawomba lipenga. Ndipo lipenga limenelo limatanthauza kwa kapolo aliyense, zinalibe kanthu ndi motalika bwanji iye wakhala akugwira ntchito ndi mochuluka bwanji iye amayenera kupitirira kugwira ntchito, pamene lipenga limenero liwomba, kapolo ameneyo ankakhala mfulu. Iye amakhoza kusiya panso khasu ndikumapita kwa ana ake. Iye samayenera kuti azigwiranso ntchito kenanso, chifukwa iye amakhala mfulu pamene lipenga lawomba. Lipenga limenero silimapereka phokoso losadziwika, koma ilo limapereka phokoso lodziwika. Ndipo munthu amatha kusiya panso chida chake, nkupita kunyumba ali mfulu ku ukapolo.

⁸⁸ Mmawa uno, Baibulo linati, “Ndipo ngati lipenga lipereka phokoso losadziwika, ndani yemwe angadziwe choti achite?” Ngati Baibulo lalalikira kuti Yesu Khristu wauka kwa akufa, Iye ali yemweyo dzulo, lero ndi kwanthawizonse, ndipo malipenga amene ife tikuwamva akuwombedwa lero akuti, “masiku a zozizwitsa anatha, palibe chinthu chonga machiritso Auzimu,” ndani yemwe angadziwe momwe angadzikonzekeretsere yekha?

⁸⁹ Chimene ife tikusoweke lero ndi amthenga odzozedwa ochokera kwa Mulungu! “Iye wauka kwa akufa! Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse!” Umenewo ndiwo Uthenga wa lero.

⁹⁰ Oh, pakhalala pali mauthenga opambana, koma Isitara waposi ena onsewo! Mauthenga opambana; Isitara inali zonse za iwo! Pamene akufa. . . anapangidwa kukonzekera kuti mdani wotsiriza. . . Ife tinawona matenda akuchiritidwa mu Chipangano Chakale. Ife tinawona zozizwitsa zikuchitidwa mu Chipangano Chakale. Panali masomphenya amene anabwera mu Chipangano Chakale. Koma munthu aliyense anakalowa

mmanda, akudabwa kuti kodi iye adzawukanso. Koma mmawa wa Isitara, pamene ophunzira amenewa analandira Uthenga wopambana umene munthu aliyense akanawumva, kodi iwo anamva chiyani? “Pitani, mukawauze ophunzira anga, Ine ndauka kwa akufa!” Imfa yagonjetsedwa!

⁹¹ Panalibepo aliyense pa dziko lapansi, panalibe mneneri, panalibe munthu wamkulu, panalibe munthu woyera amene akanatha kugonjetsa . . . Iwo akanatha kugonjetsa nthenda ndi Mzimu wa Mulungu. Iwo akanatha kugonjetsa nthawi, ndi Mzimu wa Mulungu, ndikuwoneratu zinthu zimene zimabwera. Iwo akanatha kugonjetsa zimenezo. Koma panali pasanakhalepo munthu wodzodzedwa ndi kudzodzedwa koteroko kuchokera kwa Mulungu, amene akanatha kupanga maneno amenewa, “Ine ndikhoza kuwuika Moyo wanga pansi, Ine ndidzawudzutsanso iwo. Phwasulani thupi ili, Ine ndidzalidzutsa ilo tsiku lachitatu.” Panali pasanakhalepo munthu amene akanatha kupanga maneno amenewo. Ndipo zinali zodabwitsa mmitima mwawo, ngati izi zingakhale zoonza kapena ayi.

⁹² Koma mmawa wa Isitara, iwo analandila Uthenga, “Pitani inu ku dziko lonse, mukalalikire Uthenga kwa choredgedwa chirichonse. Ine ndauka kwa akufa. Taonani, Ine ndidzakhala ndi inu nthawizonse, ngakhale mpaka kumathero a dziko lapansi. Iye amene akhulupirira ndipo nabatizidwa adzapulumutsidwa, iye amene sakhulupirira adzawonongedwa. Ndipo zizindikiro izi zizawatsatira iwo amene akhulupirira: mu Dzina Langa iwo adzatulutsa ziwanda; iwo adzayankhula ndi malirime atspano; ngati iwo adzatenga njoka kapena kumwa zinthu zakupha, izo sizidzawapweteka iwo; ngati iwo adzaika manja awo pa odwala, iwo adzachira.” *Uthenga Wa Isitara*, iwo ndi umodzi wa mauthenga odziwika amene alipo. Imfa inali itagonjetsedwa!

⁹³ Iye tikuganiza za mgonjetsi. Napoleon, pa usinkhu wa zaka sarte-firii, anali atagonjetsa dziko lapansi. Iye anagonjetsa dziko lapansi, iye anakwapula fuko lirilonse limene linkayenera kukwapulidwa. Ndipo iye anakhumudwitsidwa kwambiri chifukwa panalibenso aliyense woti amumenye, iye anakhala pansi ndipo analira. Panalibepo aliyense woti amumenye, koma iye anachita malamulo a masewero mosayenera. Makumi masauzande a mahule anawatsatira asilikari ake, iye anapita ndi mfuti ndi lupanga. Pa usinkhu wa zaka sarte-firii, iye anali atagonjetsa dziko. Koma nthawiina iye anali woletsa, ndipo iye anafa ali chidakhwa chotheratu, chifukwa iye anachita malamulo a masewero mosayenera. Iye anaiwala uthenga. Iye anali atagonjetsa, koma anaiwala uthenga. Iye anapita, koma iye anaiwala chimene iye amapitira.

⁹⁴ Monga mnyamata wamng’ono amene anathamanga mpikisano, monga momwe mpingo ukuthamangira lero, monga anthu amene akuthamanga, monga fuko likuthamangira!

Pothawirapo pathu si mabomba a atomu, pothawirapo pathu ndi Yesu Khristu ndi chiukitsiro Chake.

⁹⁵ Napoleon anaiwala chinthu chenichenicho. Chinachitika ndi chiyani kwa iye? Iye anafa atagonjetsedwa kwathunthu, chidakhwa chinachake. Chifukwa chiyani? Iye sanasewere masewerowo moyenera, ngakhale iye anali atagonjetsa dziko, mwathupi. Iye anakonzekeretsa gulu la ankhondo. Iye anali katswiri wankhondo, iye anatenga fuko lirilonse ndipo anachita zinthu (zimene iye) zimene munthu wina aliyense sakanachita kapena anayamba wachitapo, monga iye, koma iye anali ataiwala chimene uthenga weniweniwo unali. Iye anali atatenga ilo, ndipo anatenga mphamvu zake za ankhondo, koma iye anaiwala mphamvu za Ambuye.

⁹⁶ Mphamvu za Ambuye ndi chithonhozo chathu. Ife tiribe mphamvu zina. Pothawirapo pena ine ndiribe, palibe! Mulungu chitani chifundo! Tengani moyo wanga, koma musalole ine ndidzaiwale kumene kumachokera mphamvu zanga. Izo zimachokera kwa Ambuye! Ine sindikufuna zinthu zabwino za pa dziko lapansi. Ine ndikufuna Yesu, Ine ndikufuna chiwukitsiro Chake chiziyaka mmoyo mwanga.

⁹⁷ Zinali zosiyana bwanji zimenezo ndi Yesu Khristu pa sarte-firii! Pa usinkhu wa zaka sarte-firii, Yesu anali ndi chirichonse; Iye anapanga dziko lapansi. Ndipo Iye anali ndziko lapansi, ndipo dziko lapansi silinamudziwe Iye ayi. Iye sanadzipangire Yekha kukhala wotchuka mulimonse. Iye sanasonkhanitse anthu a nkhondo. Iye sanapangepo bungwe mpingo uliwonse. Iye sanadzipangire maina aliwonse aakulu kwa Iyemwini. Iye sanabwere ndi kudzitukumula kwa chiphunzitso cha madigiri chirichonse, fioloje, ndi zina zotero, panalibe cholembedwa chirichonse choti Iye anapitapo ku sukulu iliyonse ya fioloje. Koma Iye anali ndi Mulungu. Iye anali ndi Mulungu. Ndipo pa usinkhu wa zaka sarte-firii, Iye anali atagonjetsa mdierekezi aliyense amene anasuzumira mutu wake kuchokera ku gehena. Iye anagonjetsa matenda. Iye anagonjetsa zamatsenga. Iye anagonjetsa ziwanda. Iye anali atagonjetsa imfa. Ndipo pamene Iye anafa pa Mtanda, Iye anatsikira mu maenje opanda malire a ku gehena, ndipo anagonjetsa gehena.

⁹⁸ Ndipo mmawa wa Isitara Iye anagonjetsa manda. Chifukwa chiyani? Iye anasewera malamulo a masewero moyenera, anathamanga ndi Uthenga. Iye anali, Iye anapita! "Pitani." Mulungu anamutumiza Iye, ndipo Iye anali ndi Uthenga woti akawauze iwo. Ndipo ndi Uthenga umene Mulungu anamupatsa Iye, Iye anagonjetsa mphamvu za Satana. Iye anagonjetsa matenda. Iye anagonjetsa imfa. Iye anagonjetsa gehena. Iye anagonjetsa manda. Chifukwa chiyani? Iye anapita! "Pitani, mukawauze!" "Ine nthawizonse ndimachita chimene Atate Anga andiwonetsera Ine kuti ndichite. Ine sindimachita chirichonse koma chimene Iye wandiuza Ine kuti ndichite."

⁹⁹ Kenako Iye asanamwalire, Iye ananena ichi, “Ngakhale monga Atate wandituma Ine, chomwechonso Ine ndikukutumandinso inu.” Osati kuti akawumbe amuna ndi mphamvu zankhondo; osati kukaika nthawi yanu yonse mwa amene ati adzakhale Purezidenti. Izo mwinamwake zikhoza kukhala zofunikira, koma izo sizofunikira mu *Ichi*. Dziko lapansi lapita. Ife tiri ndi Uthenga umodzi, umene ndi, Yesu Khristu anawuka kwa akufa, ndipo Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.

¹⁰⁰ Dzulo, mu nyumba ya milandu yaing’ono, iwo amayesera kundipanga ine kuti ndinene chinachake chimene sichinali cholondola. Ine ndinati, “Ine si wakuba.” Ine ndinati, “Ine—ine—ine ndi woona mtima. Ndipo iwe sunganene zochuluka koma chimene chiri choonadi.”

¹⁰¹ Ndipo munthu wina anali ndi ine, anati, “Ngati munthu atayankhula ndi ine monga choncho, ine ndingamverere ngati ndiponyere bukhu pa iye.”

¹⁰² Ine ndinati, “Ayi, bwana. Ayi, kutero si bwino. Iyo si njira yake yochitira izo. Sindiko kulondola.”

¹⁰³ Iye anati, “Chabwino, bwanji inu simukudziwa kuti zinthu zimenezi zikuchitika? Bwanji inu simumakhala kunjira uko kumachita izi?”

Ine ndinati, “Ine ndimakhala nthawi yanga ndikutumikira Yesu Khristu.”

¹⁰⁴ O Mulungu, oh, anthu ndi akhungu ndipo sakutha kuwona izi! “Monga Atate andituma Ine,” Atate anamutuma Iye, Iye anapita. Iye anali ndi Uthenga woti akawauze anthu. Ndipo mu ora la imfa, Iye anagonjetsa imfa ndipo Iye anagonjetsa gehena, ndipo Iye anagonjetsa manda. “Monga Atate anandituma Ine ndi Uthenga, Ine ndikukutumani inu ndi Uthenga; osati kuti mukamange matchalitchi, mabungwe, koma pitani inu mu dziko lonse ndipo mukawonetsere Mphamvu ya Mzimu Woyera. Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira; mu Dzina Langa iwo azidzatulutsa ziwanda, azidzalankhula ndi malirime atsopano, azidzatola njoka.” Ndipo pamene matupi athu azidzapita kumanda, monga Lake linachitira, Iye anagonjetsa zonse, imfa, gehena, ndi manda. Iye ndi Mgonjetsi wamphamvu.

¹⁰⁵ Iye akutituma ife ndi Uthenga Wake. Tiyeni tizipita ndi Uthenga, tizipita ndi chinachake choti tikanene. “Pitani, mukawauze!” Osati kuthamanga ndipo kenako nkulephera kukanena, tiyeni poyamba tiwutengere Iwo mu mtima mwathu momwe.

¹⁰⁶ Pamene inu mukubwera kuti mudzapemphereredwe, mmawa uno, musabwere mwachisawawa. Mubwere ndi Uthenga mu mtima mwanu, “Ine ndine Iye amene anali wakufa, ndipo ndiri wamoyo kenanso. Ndine Amene ndinapereka Uthenga,

‘Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira.’” Ngati Mulungu Wamphamvuzonse akhoza kutenga a—a mwana wamng’ono wa maso opingasa ndikubwezeretsa kuwona kwake bwinobwino; Mulungu akhoza kumutenga mwana, a, mwana wobadwa wamwamuna, amene sanawonepo mmoyo mwake, ndi wa usinkhu wa zaka sikisitini, nkubwezeretsa kupenya kwake kwa iye; Mulungu akhoza kumutenga munthu womvetsa chisoni wodyedwa ndi khansa kotheratu . . .

¹⁰⁷ Ndipo chifukwa choti Uthengawu ndi wolondola, chifukwa choti Mulungu anawutumiza Uthenga, chifukwa choti Mulungu anatumiza mthenga, nzosakaikitsa kuti mfuti iliyonse ya gehena idzakhala ikumuwombera iye. Ndiko kulondola, iye adzapunthwa ndi kugwa, ndi kudzuka ndikugwedeza mutu wake, ndikumapitirira. Ife tiri ndi Uthenga, palibe chidzauimitse Iwo! Aleluya! “Pa thanthwe ili Ine ndidzamangapo Mpingo Wanga, ndipo zipata za gehena sizidzawugonjetsa konse Iwo.” Iwo akhoza kunena chimene iwo akufuna kunena, kuchita chimene iwo akufuna kuchita, mdierekezi akhoza kupanga ukali ndi kukuwa. Koma Yesu anawuka kwa akufa, Iye ali moyo lero mwa ife!

¹⁰⁸ Masiku angapo apitawo, ndikuyankhula kwa Doctor Lamsa wamkulu, yemwe anamasulira Baibulo kuchoka ku Aramaic, kupita ku Chingerezi. Ndipo ine ndinawona chizindikiro chaching’ono chimenecho, chizindikiro cha Mulungu pamene, chokhala ndi madontho atatu aang’ono pa icho. Ine ndinati, “Doctor Lamsa, ndi chiyani chimenecho?”

Iye anati, “Ndi Mulungu, ali ndi zikhumbo zitatu.”

¹⁰⁹ Ndipo ine ndinati, “Inu mukutanthauza, Mulungu akukhala mu maudindo atatu, monga ngati, Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera?”

¹¹⁰ Iye anadzuka ndipo anandiyang’ana ine, misonzi ikutsikira mmaso a Myuda ameneyo, iye anati, “Kodi iwe umakhulupirira zimenezo, M’bale Branham?”

Ine ndinati, “Ndi zonse zomwe ziri mu mtima wanga.”

¹¹¹ Iye anaponyera manja ake mondikumbatira ine, ndipo anati, “Ine ndinali kudabwa pamene ine ndimawona pamenepo zinthu zazikulu zikuchitika, ndi zizindikiro zimene iwe umazichita.” Anati, “Iwo amandiuza ine kuti iwe unali mneneri. Ine sindimazikhulupirira izo, kufikira panopa. Tsopano ine ndikudziwa iwe uli.” Iye anati, “Ndi zimenezotu! Umenewo ndiwo Uthenga. Chimenecho ndicho chinthu chimene chiti chidzagwedeze Ufumu wa Mulungu.” Eya. Iye anati, “Tsiku lina iwe udzafera zimenezo, mnyamata.” Anati, “Iwe udzasindikiza umboni wako ndi chinthu chomwe chomwecho.”

¹¹² Mmodzi wa anthu aakulu amene ife tiri nawo, pamene Eisenhower ndi amuna aakulu a dziko lapansi, Hollywood, mitundu yonse ya akatswiri akanema ndi chirichonse

chikuitanira pa iye, koma anakhalabe momwemo mu msonkhano. Iye anati, “Ine ndakhala zaka zina sarte zosamvetsetseka, kuchita kutanthauzira uku, osati kuchokera ku Chigriki cha ku Vatican, koma kuchokera ku Aramaic; molunjika kuchokera kumeneko, kuchokera ku Aramaic, kupita ku Chingerezi.” Ndipo iye anati, “Ine ndakhala nthawi yonse imeneyo,” iye anati, “Ine pano ndangofika mu malo amene ine ndikumuwona Mulungu wa Baibulo, akuyenda.” Iye anati, “Inu mukudziwa, M’bale Branham, ife tikhoza kuwona zizindikiro ndi zodabwitsa, koma ife timapenyetsetsa chimene Liwu la chizindikiro liri nacho. Ife Ayuda, timawona chizindikiro, koma ife timapenyetsetsa Liwu la chizindikiro.”

¹¹³ Oh, aleluya! Liwu la chizindikiro! Mulungu anamuuza Mose, “Ngati iwo sakamvera Liwu, Liwu la chizindikiro choyamba, ndiye iwo akamva Liwu la chizindikiro chachiwiri.” Osati kwambiri chizindikirocho, koma Liwu limene limapita ndi icho.

¹¹⁴ Mwaona, Myuda uja, iye ankadziwa chimene iye amachiyankhula. Iye anati, “Ine ndawonapo kuzindikira za mu mtima, ine ndawonapo zizindikiro, zodabwitsa, wakhungu akuchiritsidwa, ndi mitundu yonse ya zizindikiro zosiyanasiyana, koma ine ndimadabwa, koma tsopano ine ndikumuwona Liwu kuseri kwake sizimudula Mulungu mmagawo atatu, ndi kuti, ‘Iye ndi Mulungu mmodzi, Atate, ndipo wotsatira, Mwana...’ Iye akuti, ‘Mulungu ndi Mulungu: zikhumbo zitatu za Mulungu; maudingo atatu a Mulungu.’” Anati, “Izo zikutsimikizira zimenezo.”

¹¹⁵ Oh, m’bale, ife tiri ndi Uthenga! “Pitani, mukawauze ophunzira Anga! Ine sindine *amene* ndiri wakufa, ndi *winawake* ali pafupi kufa kwambiri, ndi *wina* ali ndi moyo. Ine ndine Iye amene Anali, amene Ali, ndi Amene Adzadza; Muzu ndi Mphukira ya Davide; Nyenyezi Yowala ndi ya Mmawa.” Inde!

¹¹⁶ Zimachita ubwino wanji kupita, kuchita ngati ungapite, ngati iwe ulibe chinachake choti ukawauze? Uyenera kukhala ndi chinachake choti ukawauze, uko nkulondola: “Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu, amakukondani inu nonse. Iye anakuferani inu nonse. Kondani Yesu Khristu Mwana wa Mulungu.”

¹¹⁷ Ndi angati anayamba akhalapo mu misonkhano, ndikumuwona zizindikiro zazikulu ndi zodabwitsa za Kwake—kuwonekera Kwake, za momwe Iye amazindikirira ndi kuwonetsera, ndi zinthu? Ameneyo ndiye Mulungu wa Kumwamba, Amene wauka kwa akufa.

¹¹⁸ Inu mukuyenera kuwona chizindikiro cha chizindikiro cha Chihebri cha Ichu. Ndi Kuwala, monga Lawi la Moto, ndipo mmenemo muli madontho aang’ono atatu, Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera, amene sanali anthu atatu. Anali Mulungu mmodzi akukhala mu maudingo atatu. Mulungu yemwe yemweyo! Aleluya! Mulungu pamwamba panu, Mulungu ndi

inu, Mulungu mwa inu. Yemweyo akudzitsanulira Iyemwini, kuwuyeretsa Mpingo Wake, kuti Iye akakhoze kukhalamo moyo. Mukamudula Iye mzidutswa, ndi kumuika mmodzi *apa*, ndi wina cha *apa*, ndi wina *apo*, izo ndi zachikunja momwe izo zingakhalire.

¹¹⁹ Ine ndikukhulupirira chiukitsiro cha Yesu Khristu, anauka kwa akufa. Ndipo Iye anali Munthu yekhayo akanakhoza kunena kuti, “Mphamvu zonse Mmiyamba ndi dziko lapansi zapatsidwa mdzanja Langa. Mphamvu zonse za Mmiyamba ndi dziko lapansi zaperekedwa mdzanja Langa. Pitani inu mdziko lonse, ndipo mukalalikire Uthenga kwa cholengedwa chirichonse.” Uthenga sunabwere mu mawu okha, koma kudzera mu mphamvu ndi ziwonetsero za Mzimu Woyera. Mulungu akuthandizeni inu kuti mukhulupirire zimenezo, Mulungu andithandize ine kuti ndikhulupirire zimenezo, ndipo ife tidzamuwona Yesu tsiku lina.

Zovuta za moyo zikadzatha,
Ife tidzamuwona Yesu pomaliza;
Pa Mpando Wake wachifumu wokongola,
Iye adzandilandira ine Kwathu,
Tsikulo likadzatha. (Uko nkulondola.)

Mchenga watsukidwa mmapazi
A Mlendo uja wa ku gombe la Galileya.

¹²⁰ Iwo anamupha Iye chifukwa Iye anadzipanga Yekha Mulungu, ndipo Iye anali Mulungu. Iwo anamupachika Iye, chifukwa, Iye anafa pansi pa chilango cha imfa. Ndicho chifukwa chake ine sindimakhulupirira chilango cha imfa. Yesu anafa pansi pa—chilango cha chilango cha imfa cha boma la asamunda la Roma. Chilango cha imfa, chinali, kupachikidwa pa mtanda. Iye anafa pansi pa chilango cha imfa, anang’amba zovala Zake kuzichotsa pa Iye, ndipo anamupachika pamenepo, anamuchititsa Iye manyazi, ndipo Iye anafa mu chikhalidwe chimenecho. Koma Mulungu anamuukitsa Iye pa tsiku lachitatu!

¹²¹ Ndipo ife ndi mboni Zake. Ndipo ngati ife sitimuimira Iye, ndani yemwe ati adzamuimire Iye?

¹²² Bambo wina anakumana nane tsiku lina, anati, “Oh, M’bale Branham, inu musamawauze. Inu musiyere kuwauza. Inu—inu mumapweteka kumverera kwa akazi, za kumakhala ndi tsitsi lalifupi, ndi zokhudza iwo kuchita *izi* ndi kuchita *izo*, ndi zina monga choncho.”

¹²³ Ine ndinati, “Ngati ine sindiwauza iwo, ndi ndani ati adzawauze iwo? Ndani yemwe ati adzanene izo?”

Anati, “Chabwino, iwe umawapangitsa alaliki amenewo kukwiya.”

124 Ine ndingakonde iwo andikwiyire ine, kusiyana ndi Iye. Icho ndi Choonadi. Uko nkulondola! [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi]. Kulondola. Ndani amene ati adzanene izo? Winawake akuyenera kuti azinene izo.

125 Yesu anati, “Pitani, mukawauze. Pitani ndipo mukawauze, mukawauze ophunzira Anga kuti ine ndauka kwa akufa. [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi]. Taonani, ine ndiri ndi inu nthawizonse, ngakhale mpaka ku mathero a dziko lapansi.”

126 Kodi inu mukukhulupirira zimenezo, abwenzi?

Tiyeni tipemphere, pamene ife tikuweramitsa mitu yathu tsopano ku pemphero.

127 O Atate Mulungu! Moonadi, “Pitani, mukawauze. Pitani, mukawauze ophunzira Anga kuti ine ndauka kwa akufa.” Ndipo Atate Mulungu, Inu simunangowauza ophunzira Anu, koma Inu munatsimikizira kwa iwo kuti Inu mwauka kwa akufa. Inu munadziwonetsera Nokha ndi iwo, ndipo munachita ndendende momwe Inu munachitira Inu musanafe. Zaka naintini handiredi zabwera ndipo zapita, Ambuye, Uthenga ukuyakabe. Iwo uli basi wowala ndi woyaka mmitima mwathu lero monga iwo unaliri ndi ophunzira amenewo, pakuti ife tikuwona Ambuye wowukitsidwa pakati pathu pomwe, akuchita zinthu zimene Iye anazichitapo kale. Ife tikudziwa kuti Iye wauka kwa akufa.

128 Isitara imatanthauza mochuluka kwa ife, chifukwa ife talowamo ndipo tikusangalala ndi chiyanjano cha chiukitsiro Chake. Pakuti ife nthawi ina tinali akufa mmachimo ndi mphulupulu, monga mwana wolowelera, koma tsopano tapeza chisomo, ndipo Mulungu watikhululukira ife machimo athu. Iye watipatsanso ife Chisindikizo, monga Iye anachitira kwa Atate Abrahamu, kukatsimikizira kuti Iye wativomereza ife. Atate Abrahamu anati iye anakhulupirira Mulungu, koma Iye anamupatsa iye chisindikizo cha mdulidwe ngati chitsimikizo kuti iye anamukhulupirira Iye. Ndipo tsopano, Atate, lero ife tadulidwa ndi Mzimu Woyera, zinthu zonse za mdziko zapita. Ife tiri ndi cholinga chimodzi: kukutumikirani Inu. Ife tiri ndi chokhumba chimodzi: kukukondani Inu, kukhala ophunzira Anu.

129 Ndipo tsopano, Ambuye, ine ndikupemphera kuti Inu mutsimikizire uthenga waung’ono woswekasweka uwu ku mtima uliwonse. Musawalole iwo kuti awuphonye iwo. Aloleni iwo awone kuti Inu muli yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, kuti Inu muli pano, mwauka kwa akufa, ndipo mudzakhala kufikira a—Mzimu ndi thupi zitalumikizanso palimodzi Pakubwera Kwachiwiri.

130 Ine ndikupempherera odwala amene ali pano, Atate, mmawa uno. Ine tsopano, mmawa wa Isitara uwu, ndaikidwa kumbali (kapena, osati kuikidwa kumbali, koma ndangoikidwa kwa kamphindi ka nthawi) mphatso zimene Inu mwandipatsa ine,

monga ngati kuzindikira za mu mtima. Dziko lapansi, ine ndakhala ndikuyendayenda kudutsa mafuko, Ambuye, iwo onse akudziwa zimenezo. Tsopano ine ndikupemphera, kuti, Uthenga umene Inu munandipatsa ine kuno kunkhalango, apo, masiku angapo apitawo, kuti, pa mphamvu yolenga imeneyo imene ili mu tchalitchi chino mmawa uno, anthu omwewo amene inalengedwerapo, Ine ndikupemphera, Mulungu, pamene ine ndikubwera kudzaika manja anga pa odwala mmawa uno, ndi abale anga pano, kuti Inu mudzagwere pa mpingo uno mmawa uno, ndi chifundo, ndi kuti Inu mukawachiritse anthu, kuti pasakhale munthu mmodzi wofooka pakati pathu pamene msonkhano uzitha. Mulole aliyense wa iwo adalitsidwe ndipo achiritsidwe.

¹³¹ Ife tikuzindikira, Ambuye, si chinthu choti ife tingachichitepo mwaife tokha. Ndi chophweka ngati chikhulupiriro cha mwana, kukhulupirira. Ife tikutha kuwona ophunzira iwo atapatsidwa mphamvu yochiritsa odwala, iwo anapita patsogolo ndipo iwo anagonjetsedwa ndi nthenda ya khunyu; akufuula ndi kulira, mwinamwake, ndi kumalumphalumphu, ndi kuyesera kuti amuthamangitse mdierekezi ameneyo. Koma pamene iye anadzakumana ndi Yesu, oh, zinali zosiyana bwanji! Iye anati, “Iwe mzimu woipa, tuluka mwa iye.” Ndi zosiyana bwanji! Oh, iye anadziwa kuti ameneyo sanali mtumwi. Ameneyo anali Ambuye Mwiniwake. Ndipo mzimu unamung’amba mnyamatayo ndipo unamuponyera iye pansi. Koma Yesu anati, “Iye sanafe. Mungomutenga iye ndipo mukamupatse iye chakudya.” Mzimu woipa unali utamuchokera iye.

¹³² O Yesu, Inu Mwana wa Mulungu, bwerani kenanso, mudzawudzoze Mpingo Wanu momasuka, mwathunthu, mwamphamvu. Mulole Mzimu wa Yesu wamoyo woukitsidwa uwukitse mpingo waung’ono uwu mmawa uno mu chikhulupiriro chatsopano, mphamvu, mphamvu ya chikhulupiriro, kuti ife tikathe kuchititsa manyazi wotsutsa aliyense. Perekani izi, Ambuye. Ndikuwapereka anthu onsewa kwa Inu, kupempha kuti Inu muwadalitse iwo ndi kuwapatsa iwo chipulumutso ku miyoyo yawo, machiritso ku matupi awo, kudzera mwa Yesu Khristu Ambuye wathu.

¹³³ Ndipo ndi mitu yathu yoweramitsidwa, ine ndikufunsani funso. Alipo winawake pano amene sali Mkhristu, angafune kuti akumbukiridwe tsopano, ndipo akuti, “Ndipempherereni ine, M’bale Branham”? Mulungu akudalitseni inu pamenepo. Winawakenso, “Ine si Mkhristu. Ine ndamva nkhani kuti Yesu anauka kwa akufa, koma ndithudi ine sindikuzidziwa izo. Iye sanaukepo mu mtima mwanga. Ine ndiliba kukhutitsidwa. Ine ndikudwala, nanenso. Ine ndiyenda kudutsa mzere wa pemphero, kubwerera ndi kudzadutsanso wina, kubwerera ndi kudzadutsanso wina. Ine ndizipita tchalitchi ndi tchalitchi, ndi

malo ndi malo.” Sindizo ayi. Ndi kumukhulupirira Iye. Iye anauka kwa akufa. Izo zikhazikitsa izo. Winanso mungakweze dzanja lanu? Munene. . . Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu. Winanso, “Ine ndikufuna kuti ndikhulupirire. Ine ndikufuna kuti ndikhulupirire?”

¹³⁴ Ndi angati amene akudwala muno? Kwezani dzanja lanu, ndikuti, “Ine ndikufuna kuti ndikhulupirire. Ine ndikufuna kuti ndidziwe Uthenga mmawa uno.” Mulungu akudalitseni inu. Ndizo zabwino. Inde, Mulungu akudalitseni inu, mwana. Zabwino. Chabwino.

¹³⁵ Tsopano, Teddy, ine ndikufuna iwe uyimbe “*Msing’anga Wamkulu,*” miniti chabe, ngati ungate, “tsopano ali pafupi.” Ndipo pamene iwe ukuchita zimenezo. . .

¹³⁶ Izo ndi zovuta tsopano. Masomphenya akuwoneka paliponse mchipinda muno, mwaona. Eya, ine ndikuyesera kutero, ine ndimayesera kuzipanga izi kuti zikhale chiwukitsiro, mwapamwamba pang’ono, mwapamwamba pang’ono kuchoka ku—kuchoka pa mulu wa phulusa pamene ine ndakhalapo. Ine ndikufuna vumbulutso lowonjezera pang’ono. Ine ndikudziwa chinthu chimodzi: Ngati ine ndizigwiritsitsabe ku utumiki woyamba uja, wachiwiriwo subwera, iwo sunabwere. Tsopano ngati ine ndizigwiritsitsa ku wachiwiri, wachitatu subwera, mwaona. Ine ndikuyenera ndisunthepo, ndisunthepo ndi kukhulupirira izo, “Mulungu ananena chomwecho!” Masiku pang’ono apitawo. . .

¹³⁷ Tsopano inu mukhoza kudzutsa mitu yanu ngati inu mukufuna kutero. Ine ndinawawona manja anu; Mulungu anawawona iwo.

¹³⁸ Ine ndikufuna ndikuuzeni inu chinachake chaching’ono. M’bale Ed Daulton, ine ndikukhulupirira iye anangobwera pakhomo, m’bale wabwino wa Baptisti, iye ndi mkazi wake. M’bale Jeffries ali muno penapake. Othel Jeffries. Ndipo iye ali muno, ine ndikudziwa iye ali muno penapake. Komabe, abale amenewo anakonza msonkhano kuti ine ndipiteko, kumusi mu Kentucky. Abale, abale ofunika, okonda oyandikana nawo ndi anthu awo. Iwo ali ndi zipinda zoyankhuliramo ndi zipinda zosungiramo zida zankhondo ndi zinthu, basi kwa msonkhano wa usiku umodzi, iwo anabwereketsa zida zankhondo. J. T. Hoover wamng’ono, chonse chimene chake. . . L. G. Hoover anakonza umodzi kumusi mu Elizabethtown. Ndi M’bale Ed Daulton komwe ku Willow Shade kapena—kapena Somerset, Somerset. Ndi m’bale, m’bale winayo anali kumusi kuzungulira Glasgow, kumene ine ndinabwadwirako. Anthu a kumeneko kumene ine ndinabadwirako ndi kuleredwerako, kumene Mngelo wa Ambuye anawonekera koyamba kwa ine.

¹³⁹ Ndipo ine ndinkafuna kuti ndibwerere. Koma ine ndinamverera kukoka pang’ono. Ndipo ine ndinati, “Chabwino,

chifukwa cha abale, ine ndidzakonza msonkhano.” Mwamsanga nditangofika mu chigwa chimenechi, kummero kwanga kunatsekeka pomwepo ndipo ine sindinayankhule kwa masiku naini, kufikira misonkhano itadutsa.

¹⁴⁰ M’bale Ruddell, iye akhoza kukhala ali muno mmawa uno, nayenso, mmodzi wa abale kuchokera pa kachisi uyu, iye ndi Junie Jackson ndi iwo, ine ndimayenera kukakhala ndi msonkhano wa iye. Ndipo pomwepo, kummero kwanga kunatsekeka. Ndipo chinthu choyambirira inu mukudziwa, ine ndinatentha mthupi pafupifupi handiredi ndi faivi. Ndipo ine ndimapita ku msonkhano, poyamba, ndipo—ndipo Doc Schoen ananena ndi ine...ine ndinati, “Kummero kwanga mawu asasa.”

¹⁴¹ Iye anati, “Ine ndikupatsa iwe chinachake choti chimasule kholinga limenelo, ndipo iwe upitirire ndipo ukalalikire.” Ndipo ine ndinamwa chinachake chimzake chimene iye anandipatsa ine, ndipo, chimene icho chinali, icho chinakoka nkhwiko imeneyo ndipo chinayitseka iyo. Kenako ine ndinagona pa bedi kwa masiku naini, ndi kutentha kwa mthupi kwakukulu.

¹⁴² Ambiri a abale anga pano anabwera kwa ine, ambiri a abale otchuka anabwera kudzandipempherera ine. Apa panabwera M’bale Graham Snelling, apa panabwera M’bale Ruddell, ndi abale onsewa apa, onse anasonkhana mkati, akupemphera ndi china chirichonse. Ine ndikupemphera, ndikuyesetsa mwakukhoza kwanga, sindimatha ngakhale kunong’ona. Ine ndinadabwa, “Kodi izi ndi chifukwa chiyani?” Mkazi wanga wamng’ono wokonedwa atakhala pamenepo, iye ndi iwo akundipempherera ine, basi zimangopitirira kukhalabe basi chimodzimidzi. Iwo samatha kumvetseta.

¹⁴³ Tsopano, iye anandipatsa ine mankhwala ena kuti ndimwe, koma ine sindinawamwe iwo, chifukwa anali oledzeretsa ubongo. Ndipo kenako ine ndinangozisiya izo zipite. Ndipo ine ndinangopitirira kumaganiza, “Ambuye, ndithudi!”

¹⁴⁴ Ndipo kenako, misonkhano yonse itatha, Lolemba (uwo unali, msonkhano wotsiriza, umayenera kukhala Loweruka), ndipo kenako (ine ndikukhulupirira), ndipo kenako, Lolemba ine ndinayesera kudzuka. ine ndinali wofooka kwambiri, ine sindimatha kuyenda mchipinda. Ine ndinakhala pansu.

¹⁴⁵ Inu mukudziwa, ndine wothokoza kwambiri chifukwa cha mkazi woperekedwa ndi Mulungu. Sichoncho inu, abale? Mkazi weniweni, mzako weniweni!

¹⁴⁶ Ine ndinakhala pansu. Ine ndinamukodola iye, ndipo ndinamupanga iye abwere moyandikana nane. Ndipo ine ndinati, “Meda, nthawizina ine ndimadabwa,” Ine ndinati, “Ine ndimadabwa, vuto ndi chiyani.” Ine ndinati, “Nchifukwa chiyani misonkhano imeneyo inakhalapo, ndipo Mulungu nkundilola ine ndigone monga chonchi?” Ine ndinati, “Chifukwa chiyani

zinakhala chomwecho?” Ndipo ine ndinati, “Nthawizina ine ndimadadwa ngati Iye anandiitana ine nkomwe.”

¹⁴⁷ Iye anati, “Kodi iwe sukudzichitira wekha manyazi?” Mukuona? Ndipo iye anandiuza ine, anati, “Bill, kodi iwe sukudziwa kuti Mulungu akudziwa chimene Iye akuchita ndi iwe? Basi, ungokhala chete.”

¹⁴⁸ Ndipo chotero ine ndinalowa mkati. Izo zinakhala ngati zinandidzudzula ine pang’ono, inu mukudziwa. Ndipo chotero ine ndinalowa mkati ndipo ndinadzagona pa bedi. Iye anadzalowa kuti adzasinthe zofunda. Ndipo iye anali atatenga zi—zinthu pa nkono wake, ndipo pamene iye anayamba kutuluka, ine ndinayang’ana, ndipo pamenepo panali . . .

¹⁴⁹ Ine ndinawona pa- . . . chinyumba chachikulu chosungiramo zida zankhondo, chimene dzuwa linadzawalira pansi ndipo linaphulitsira icho pansi, kuchiphulitsa icho mzidutswa, dzuwa likuwala kuchokera Kumwamba. Ndipo pamenepo panadzabwera azimayi awiri ndi mzibambo, anabwera. Ndipo iwo anali nato kunjako ngati tina tating’ono, ngati tating’ono . . . mtundu wina ngati mifuti yaing’ono yowomberera, chomwecho. Ndipo iye anati, “Izo zikukhomerera misomali.” Ndipo anati, “Ife ti . . . Iwe ugwire zidutswa izi, M’bale Branham, ndipo ife tikumangiranso iwe nyumba yosungiramo zida zankhondo imeneyi.”

Ndipo ine ndinati, “Chabwino, ine ndichita zimenezo.”

¹⁵⁰ Koma Chinachake chinati, “Iwe usachite zimenezo.” Chabwino, ine ndinaweramira pansi kuti nditenge chidutswa, monga *chonchi*, kuti ndichimange icho monga *chonchi*. Ndipo basi kenako Liwu linayankhula kwa ine, ndipo linati, “Tsopano iwo ali pa msewu kuti adzakutenge iwe kuti ubwerere. Iwe usakhulupirire zimenezo.” Linati, “Iwo nthawizonse amakhala odzipereka, ndipo iwo akubwera kwa iwe ndi PAKUTI ATERO AMBUYE, koma iwo akulakwitsa.” Mukuona?

¹⁵¹ Fred Sothmann, ambiri a iwo muno, anali pamenepo pamene ine ndinawauza iwo zokhudza izo. Pasanathe ora limodzi, anthu anayendetsa kufika pa khomo langa. Ine ndinati, “Pali azimayi atu ndi mzibambo.”

“Ndizo ndendende kulondola.”

“Iwo abwera ndi PAKUTI ATERO AMBUYE?”

“Inde, bwana, iwo . . .”

¹⁵² Ine ndinati, “Ndithudi, inu mukudziwa choti muwauze iwo.” Odzipereka molakwika, mwaona. Anthu abwino, koma odzipereka molakwika. Mukuona?

¹⁵³ Kenako ine ndinaganiza, “Chabwino, kodi ine ndichite chiyani? Ine ndiyenera ndichite chiyani?” Ndipo kenako Meda anadzalowa, ndipo iye anali atabwerera. Ndipo M’bale Freddie anapita ndipo anakawauza anthuwo. Ndipo kenako

patapita kanthawi, ine ndinali mmenemo pa—pa bedi, ndipo ine ndinaganiza, “Nchifukwa chiyani izo zimachitika chomwecho? Chifukwa chiyani ine sindikutha kuyankhula? Nchifukwa chiyani ine sindikutha kuyankhula ndi winawake, kapena chinachake?” Ndipo ine ndinali nditagona pamenepo. Ndipo Meda anadzalowa, ndipo ine ndimabwerera kutuluka mchipindamo.

¹⁵⁴ Ndipo ine ndinayang’ana, ndipo ine ndinawona chinachake chikuzimilira kumbali imodzi. Ndipo ine ndinayang’ana, ndipo pamenepo panali ichi...khoma langa linatseguka, ndipo ine ndinamuwona Yesu. Ndi angati a inu munandimvapo ine ndikunena kuti ine ndinamuwona Yesu kawiri mmoyo wanga, mu masomphenya? Ndipo ine ndimakhulupirira ine ndikanadzamuwona Iye kenanso mapeto a nthawi asanafike, mwaona, kudzamuwona Iye kenanso. Tsopano, ine ndinayang’ana, ndipo mlengalenga munali pomwe apo, zimangowoneka ngati kuti ine ndimayang’ana kudutsa khoma. Ndipo pamenepo panali Baibulo litaima monga *chonchi*, Baibulo lalikulu lopambana litaima mu mlengalenga. Chabwino, panali chinachake chinadzawalapo mozungulira Baibulo, ndipo kuchokera mu Baibulo munatuluka mtanda wa golide wokongola kwambiri zedi. Ndipo iwo unadzaima monga *chonchi*, ndipo kuwala kukubwera kuchokera konsekonse mozungulira iwo, ndipo kutuluka mu mtanda umenewo Iye anabwerapo. Baibulo limanyezimiritsa mtandawo, mtandawo umanyezimiritsa Iye. Ndipo Iye anabwera akuyenda, ndipo anadzayenda kufika pamene ine ndinali. Ine ndikutha kuziwona izo powonekera basi, ine ndikutha kuwona mtanda umenewo ukunyezimiritsa tsitsi Lake ataima pamenepo, ataweramitsa pa nkhope Yake.

¹⁵⁵ Iye anayang’ana pansa kwa ine monga *choncho*, ndipo Iye anati kwa ine, “Iwe ukudikirira utumiki wako watsopano kuti utsimikiziridwe kwa iwe.” Iye anati, “Ine ndawutsimikizira kale iwo kwa iwe. Iwo watsimikiziridwa kale. Iwe ukuyenera kuti uvomereze iwo.” Mukuona? Ndipo ine ndinaima ndipo ndinamvetsera kwa Iye miniti chabe. Ndipo izo zinabwera mmalingaliro anga. Ine sindinazimvetsera izo, izo zinangobwera mmalingaliro anga.

¹⁵⁶ Ngati munthu yemwe wakhala ali wochimwa moyo wake wonse, ndipo iye akudziwa kuti pali Baibulo, akudziwa kuti kuli Mulungu, koma zonse mwakamodzi iye akumva ulaliki, ndiye Chinachake chikumuuza iye, “ndi iweyo.” Ndiye, Mawu omwewo akhala ali pamenepo nthawi yonse, komabe iwo atsimikiziridwa kwa iye, ndiye iye amati, “Ambuye, ndikhululukireni ine.” Koma izo sizichita ubwino uliwonse kufikira iye atavomereza chipulumutso chake, kenako iye amapita kunja ndipo iye amakhala Mkristu. Ziribe kanthu kuti

iye alira mochuluka bwanji, apempha mochuluka bwanji, iye akuyenera kuvomereza Izo.

¹⁵⁷ Ndipo Iye ananena kwa ine kenako, “Iwe ukuyenera kuvomereza izo mwanjira yomweyo. Iwe ukuyenera kukhulupirira izo.”

¹⁵⁸ Ine ndimachita mantha ndi kugonjetsedwa. Chirichonse, ine ndimawopa kuti ndibweretsa chitonzo. Ine nthawizonse ndimachita mantha ndi zimenezo, ndimayang’ana, kuganiza kuti ine nditchula chinthu cholakwika. Chifukwa, ine ndatenga chenjezo la Baibulo, momwe kuti Mose anapatsidwa mphamvu yaikulu, ndipo iye anakantha thanthwe mmalo moyankhula kwa ilo. Ine ndikukumbukira za Eliya, chifukwa iye anali wadazi, ana aang’ono amenewo akumunyoza iye chifukwa chokhala wadazi; ndipo iye anayika themberero pa ana amenewo, ndipo forte-thuu a iwo anaphedwa ndi zimbalangondo, mwaona. Ndipo umenewo sunali Mzimu Woyera, koma anali mneneri ameneyo, atakwiya. Ndipo ine—ine ndadutsa mu zinthu zonsezo, kufika ku chimenecho.

¹⁵⁹ Ndipo pamenepo Iye anaima, akuyankhula ndi ine. Ndipo Iye anati, “Koma iwe ukumayenda ndi ambiri.” Iye anati, “Kuti uyende ndi Ine, iwe uziyenda wekha.”

¹⁶⁰ Ine ndinali nditawona pamenepo, ine ndinali ndikutengeka kwambiri ndi zipembedzo ndi chirichonse, inu mwaona, winawake kumayesera kukuuza iwe choti uchite ndi choti usachite. Iwe ukuyenera kumutsatira Iye. Tsopano, kumbukirani masomphenya amene Iye anandipatsa ine okhudza nsomba, inu mukudziwa, ndi momwe kuti iwe sukanaphunzitsa zizindikiro zauzimu kwa makanda a Pentekoste. Inu mukukumbukira. Ndipo izo zinali pamenepo. Ndipo ine ndiri mphepete mwenimweni mwa Uthenga uwu watsopano.

¹⁶¹ Mosakhalitsa momwe masomphenyawo asanandichokere ine, ine ndinati, “Ameni, Ambuye!” Ndipo mkazi wanga anali ataima pamenepo, pafupi kukomoka. Ndipo ine ndinadumpha kuchoka pa bedi, ndipo ine ndimatha kuyankhula bwino bwino monga momwe ine ndinkachitira. Mu mphindi chabe, kutentha thupi kulikonse kunandichokera ine.

¹⁶² Ine ndinamuitana Doc Schoen, ine ndinati, “Ine ndikufuna kuti iwe undiyang’ane ine.”

Iye anati, “Chiyani?”

¹⁶³ Ndipo ine ndinapita kumeneko, ndipo iye anandiyang’ana ine, anayang’ana kudzera mu nkusani mmenemo, anati, “Ndiuzeni ine chachitika ndi chiyani, M’bale Branham.”

Ndipo ine ndinati, “Iwe ungakhulupirire nkhani yanga?”

Iye anati, “Ine ndingakaikire bwanji iyo? Iyo yachitika.”

¹⁶⁴ Ndi zimenezotu, mwaona. Ndi zimenezotu, mzanga. Mulungu amadziwa momwe angakugwirire iwe pa mulu wa

phulusa. Iye amadziwa momwe iye angachitire chinachake kwa iwe mpakana Iye atafikitsa Uthenga kwa iwe, mwaona, kuti akathe kuchita chinachake.

¹⁶⁵ Lero, ine sindikudziwa ndikugonjetsedwa kungati. Ine ndinakalowa mkati osati kale kwambiri, ndimamvetsera kuwulusa kwa pawalesi. Ndipo pamenepo panali mtumiki akulalikira za chiukitsiro, kuchokera ku Akorinto Woyamba 15. Ndipo iye amalalikira chiukitsiro. Ndipo iye anadzaima pakati penipeni pa ulaliki wake, ndipo iye anati, “Inu mukudziwa, anthu ambiri amawopa kugonjetsedwa.” Iye anati, “Pamene General Patton anataya gulu la asilikari,” anati, “ndiye iwo anamuzi iye. . .Iye anawabweza ndipo iye amafuna ena owonjezera, ndipo iwo anatumizako ena ambiri. Iye anawapha iwo, ndipo iye anayitanitsa ena owonjezera. Ndipo pamene iye anawapeza iwo gulu lachitatu kumtunda kumeneko,” anati, “nthawi iliyonse chipolopolo chikalira, iwo amathamangira pansu pa chitini, kapena kuthamangira pansu pa chinachake, akuwopa.”

¹⁶⁶ Iye anati, “Munditumizire ine amuna, osati ana.” Iye anati, “Ine ndikufuna amuna amene ali okonzeka kuti afe. Ine sindikufuna winawake amene akuwopa kufa. Ngati chifukwa chimene ife tikumenyanirana sichiri choyenera kuchifera, ndiye muwachotse iwo akhale kutali ndi ine. Ine ndikufuna amuna.”

Iwo anati, “Koma iwe walephera nkhondo ziwiri kapena zitatu.”

¹⁶⁷ Iye anati, “Ine sindinalephere nkhondo. Ine ndangolephera ndewu.” Chinachake chinayankhula mu mtima mwanga.

¹⁶⁸ Ine ndikukumbukira Eisenhower anati, “Pamene ine ndinaponya chipolopolo, ndikulamula ndipo iwo anadzawombera chipolopolo mu mfuti, Iwo anakhethemula icho ndipo kunali kuphulika, icho sichinagwire ntchito,” anati, “Ine sindinasiye ndi kungogonja. Ine ndinachotsa chipolopolocho ndipo ndinadzaikamo china mmenemo, ndinaiyesa iyo. Icho chikapanda kugwira ntchito, ine ndimaika china mmenemo, mpaka chimodzi chitagwira ntchito.”

¹⁶⁹ Umo ndi mmene izo zikuyenera kuchitidwira. Ine sindikudziwa momwe izo zitakhalire. Koma Mulungu ngati Woweruza wanga pa guwa ili, ine sindikudziwa ndi kuphulika kungati ndi kungati—kumenyana kungati komwe ine nditagonje, koma ine sindigonja nkhondoyo. Iye anandiuza ine kuti Iye adzakhala ndi ine. Ine ndiimabe mpaka nditawona utumiki umenewo utatsimikiziridwa ndi kuwuwona iwo ukuchitika. Ine ndikuyamba mmawa uno, mwa chisomo cha Mulungu. Ine sindikudziwa ngati izo zitagwire ntchito kuno, kaya izo zitagwira ntchito kwina kwakenso, momwe izo zitagwirire ntchito kapena chimene chitachitike. Koma ine ndiyenda kutsika mmizere ya pemphero, kupempherera odwala, kufikira

ine osadziwa chimene chikuchitika. Ine ndinaziwonapo izo zikuchitika kawiri kapena katatu.

¹⁷⁰ Ine ndinaziwona izo zikuchitika mu nyumba ya Hattie. Ndi angati amene anamvapo nkhani ya agologolo, ndi za mtsikana, mkazi wamng'ono? Munthu woyamba mu zonsezo chiyambireni ife kudziwa, kuyambira mmasiku a ophunzira, anayamba wapatsidwapo mwayi wonena, "Pempha chimene iwe ukufuna," pamene iwe uli pamenepo. Kodi inu munayamba mwamvapo nkhaniyo? Kodi inu munayamba mwamuwonapo mkaziyo? Ndi angati amene sanamuwonapo iye, ndipo akufuna, angakonde atamuwona mkaziyo amene zinamuchitikirayo? Ife . . .

Hattie, kodi ungaimirire? Ndi ameneyo donayo.

¹⁷¹ Nditayima mnyumba yake. Nditatha kuwawona agologolo eyiti, kumene kunalibiretu mwamtheradi aliyense pozungulira paliponse, ndipo, kungoyankhula mawu, ndipo pamenepo iwo anapezeka ataima pamenepo. Izo nzoona. Ndizo, pamenepo iwo anali. Ndipo ine ndinati, "Nchiyani chinawapangitsa agologolo amenewo kuti abwere pamenepo?" nditakhala pa tebulo lake. Ndipo amayi ake, Mlongo Wright, apa pali M'bale Wright, anali atakhala pamenepo. Ndi angati amene anali pa tebulo pamenepo, ndi angati ali muno mmawa uno? Kwezani mmwamba manja anu. Chabwino, ndi awo pamenepo, konse konse mchipindachi. Mukuona? Chabwino, iwo anali pamenepo. Ndipo ine ndinati, "Tsikulina. . ." Mlongo wawo wamng'ono wolumala atakhala pamenepo.

¹⁷² Ine ndinati, "Izo zikuyenera kubwera mwa masomphenya, zina zotero, koma tsikulina izo zidzabwera mosiyana." Ndinali kuyankhula monga choncho. Zonse pakamodzi, Chinachake chinadzodza zimenezo (chisiyireni icho kwa anthu awa), Ine sindinamvererepo kudzodza kwangati kumeneko. Chifukwa chiyani? Chifukwa Hattie ananena chinthu cholondola.

¹⁷³ Ine ndinati, "Kodi agologolo amenewo akuchokera kuti? Panalibepo aliyense pamenepo, panalibe ngakhale malo a iwo, chimodzimodzi ngati pa pholo ya telefoni pamenepo. Ndipo ine ndinawona izo zikuchitika nthawi eyiti zolunjika." Ndipo ine ndinati, "Ine sindikudziwa kumene iwe achokera." Ine ndinati, "Chinthu chokhacho chimene ine ndikudziwa, ndi chakuti Mulungu anayesera kuti atsimikizire Uthenga kwa Abrahamu nthawi ina, ndipo Iye anayankhula mwanawankhosa nkukhalapo, chifukwa Iye ankafuna mwanawankhosa, kuti atsimikizire Izo. Izo zikuyenera kukhala kuti ine ndimasowekera gologolo, kuti ndimuyankhule wanga. Ndipo Iye anachita izo nthawi eyiti zolunjika, kapena nthawi seveni zolunjika, kani, nthawi seveni zolunjika." Ndipo ine ndinati . . .

¹⁷⁴ Ndipo, Hattie, mwinamwake osadziwa chimene mkaziyo amayankhula. Taonani momwe Izo zinawalambalalira olemera ndi odzikweza. Taonani momwe Izo zinalambalalira chirichonse,

ndikubwera kwa mkazi wosauka wamng'ono wokalamba mdziko mmenemo.

¹⁷⁵ Ndipo ine ndinali ndi madolla twente mu thumba langa, kuti ndimubwezere mkaziyo, kuti, iye anali atalonjeza ma dolla fifite pa tchalitchi chatsopano ichi chimene chikumangidwa. Ndipo ine sindikunena izi kuti ndimuchititse iye manyazi; iye sakanakwanitsa ma centi fifite, ndithudi, kuti apereke izo. Koma, mtima wake mu Uthenga, iye amafuna kutero. M'bale Neville, ine ndikukhulupirira, anali atavomereza izo, sakanakhoza kutenga zina zonsezo, anangomulola iye apereke ma dolla twente a izo. Ndipo ine ndinali ndi ma teni dolla awiri mthumba mwanga, Meda anali atandipatsa ine kuti ndikagule zapanyumba, ndipo ine ndinati, "Ine ndikamubwezera iye lero."

¹⁷⁶ Kenako ine ndinaganiza, Chinachake chinayankhula ndi ine, chinati, "Yesu anamuwona mkazi wamasiye ameneyo akuika masenti ake atatu, ndipo Iye sanakamubwezere iye." Iye anamulola iye apitilire chifukwa Iye anali ndi chinachake chachikulu kumusi kwa njirayo.

¹⁷⁷ Sindinadziwe mpang'ono pomwe kuti Iye amayankhulana ndi ine mwanjira yomweyo, za mkazi wamasiye, wopanda mwamuna. Mwamuna wake anaphedwa. Komanso ine sindinadziwe kuti ameneyo anali Yemweyo, pamene ine ndinati, "Ndiye ine ndingosunga ma dolla twente, Inu muli ndi chinachake cha iye."

¹⁷⁸ Ine ndinati, "Chinthu chokha chimene ine ndikudziwa, kuti Yehova adakalibe Yehova-Yire. Iye ndiwothekera kupereka nsembe."

¹⁷⁹ Ndipo Hattie, osadziwa chimene iye amanena, iye anadzuka ndipo anati, "Zimenezo si china koma choonadi, M'bale Branham." Oh, mai! Chimenecho chinali chinthu choyenera kunena. Chimenecho chinali chinthu choyenera kunena.

¹⁸⁰ Pa nthawi imeneyo, Mphamvu ya Mulungu inakhudza malo amenewo; ine sindinamvererepo kudzodza koteroko. Pamene Iko kunatero, ine ndinati, "Hattie, PAKUTI ATERO AMBUYE, pempha chimene iwe ukufuna! Ine sindikusamala chimene icho chiri, Mulungu wandipatsa ine ulamuliro kuti ndikupatse iwe chokhumba cha mtima wako pompano. Ngati iwe ungapemphe ma dolla miliyoni, iwe ukhala nawo. Upemphe za mtsikana wamng'ono wolumala uyo kuti adzukepo ndi kuyenda, iye akhala nazo izo. Upemphe china chirichonse."

Iye anati, "Ine ndipemphe chiyani, M'bale Branham?"

¹⁸¹ Ine ndinati, "Chirichonse chimene iwe ukufuna. PAKUTI ATERO AMBUYE." Oh, ndi kumverera kotani!

¹⁸² Iye anayang'ana pozungulira. Apo panakhala bambo wake wa imvi mmutu amene anabwerera kwa akufa, pafupifupi. Apo

panakhala amayi ake achikulire, wodwalika. Apo panakhala mchemwali wake wamng'ono, wolumala.

183 Koma iye anasankha basi chimene chinali cholondola. Iye anali ndi anyamata awiri a usinkhu wa mmatini basi pa usinkhu wolekerera uwo. Mwamuna wake wofunikira anapita ku Ulemelero; iye anali Mkristu, akudikirira. Koma anyamatawo sanali Akristu. Iye anati, "Miyoyo ya anyamata anga awiri." Mulungu adalitse mtima wake.

184 Ine ndinati, "PAKUTI ATERO AMBUYE, iwe wapatsidwa iwo."

185 Ndipo ndi awa ali apa, anabatizidwira mu Chikhulupiro. Iwo amandiiza ine usiku wina, ngakhale, mnyamata wamng'ono kwambiri ameneyo akutsuka mapazi mmenemo, anaika manja ake pamutu pa M'bale Neville, ndi kumupempherera iye pamene iye anali kutsuka mapazi.

186 Anyamata aang'ono awiriwo mwinamwake akhala muno mu msonkhano penapake mmawa uno. Iwo alipo, Hattie, kodi iwo ali muno ndi iwe? [Mlongo Hattie akuti, "Iwo ali kumbuyo kumeneko."—Mkonzi]. Kumbuyo, kumbuyo. Inu muli pati, anyamata? Kwezani mmwamba manja anu. Ali kuti anyamata awiriwo? Ndi awo pamenepo, ayima kumbuyo mmbuyo. Mulungu akudalitseni inu. Chabwino. Ndi inu pamenepo.

187 Tsopano, chinachitika ndi chiyani? Chinthu chomwe chomwecho, ziribe kanthu chiyani, iye akanapezeka... chimene iye akanachifunsa, iye akanakhala nacho icho. Iye akanachilandira icho.

188 Tsopano ine ndikufuna kuwona icho chikuchitika. Icho chikhala kawonedwe ka anthu pa Uthengawu. Mwaona momwe iye ananenera izo? Iye anangonena chinthu cholondola. Ndi chimene inu munena, chimene chimachita izo. Chimene inu munena!

189 Tayang'anani pa mkazi Wachisurofonika pamene iye anabwera kwa Yesu. Iye anati, "Ambuye, mwana wanga wamkazi wagwidwa ndi chiwanda kwambiri. Inu Mwana wa Davide, mubwere mudzamuchiritse iye."

190 Iye anati, "Si chabwino kwa Ine kutenga mkate wa ana ndi kuwupereka iwo kwa inu agalu."

191 Psyii! Nanga bwanji ngati Iye akananena zimenezo kwa ena a ife? Ife tikanati, "Kunditchula ine galu? Huh, panalibe kanthu kwa Iye, mulimonse! Mpingo waukuluwo ukulondola. Iye sali kanthu koma woyera wodzigudubuza. Iye sali kanthu koma Bezebule." Ife tikanakhala ndi mawonedwe amenewo. Koma osati iye.

192 Iye anati, "Ndi zoonu, Ambuye. Inu mukulondola ndithudi. Koma agalu ndi wololera kudya nyenyetswa za pansu pa tebulo la ana."

¹⁹³ Zimenezo zinamupeza Iye. Iye anati, “Chifukwa cha mayankhulidwe awa, chiwanda chamuchokera mwana wako wamkazi. Chifukwa cha mayankhulidwe awa!”

¹⁹⁴ Ndi mawonedwe anu, abwenzi. Kodi Iye sanazinene izo? Inu mukuyenera kukhulupirira izo, abwenzi. Inu, musandikhulupirire ine, ine ndi munthu; koma inu mukhulupirire zimene ine ndikukuuzani inu, mukhulupirire Uthenga. Ngati inu simukumukhulupirira mtumiki, mukhulupirire Uthengawo. Ngati munthu akanalowa mchipinda mmenemo, ndi telegalamu, ziribe kanthu kuti ndi ndani, momwe munthuyo amawonekera kapena amene iye anali, wamkulu kapena wamng’ono, inu mukhulupirire zimene ziri pa telegalamuyo, osati munthuyo. Mulungu anandituma ine kuti ndidzakuuzeni inu. Ine ndiri ndi Uthenga. Mulungu anandituma ine kuti ndidzakuuzeni kuti Iye wauka kwa akufa, kuti Iye ali pano mmawa uno. Iye wazitsimikizira izo mwa zizindikiro ndi zodabwitsa, kuti Iye ali pano, ndipo aliyense wa inu akhoza kuchiritsidwa ku nthenda zanu ngati inu mungangotenga mawonedwe oyenera pamene inu mukhale mukubwera. Kodi inu muchita zimenezo, pamene ife tikuimba *Kungo Khulupirira*.

¹⁹⁵ Tsopano mulole iwo amene ati apemphereredwe, abwere kumtunda kuno ndi kudzapanga mzere mozungulira pano. Tsopano, musabwere pokhapokha inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse.

¹⁹⁶ Ambuye wofunika, ora lija ndi lino. Ine ndikupemphera kuti Inu muwachiritse anthu awa, Ambuye. Ndipo muyeretse mafuta awa. Mutenge ulemelero kwa Inumwini, Atate. Ife tikutumiza izi mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

¹⁹⁷ Ine ndikudabwa ngati ife tingafunse kuti anthu awo amene aima ku mbali *iyi* kuno, ngati pali njira yoti iwo angopeza mpata malo aang’ono apa, kuti ife tikhoze kudutsitsa anthu, ngati inu mungatero. Tizidutsa pomwe apa, kutulukira mbali *iyi*. Ndiye iwo onse akhoza kumadzera mbali *iyi*, kumatsika ndi mzere, kuti tipange mzere umodzi wotulukira mbali *iyi*.

¹⁹⁸ Chinachake chikuyenera kuchitika, M’bale Neville. [M’bale Neville akuti, “Ameni. Izo zikuchitika pakali pano. Ambuye alemekezeke! Yesu ali pano. Inde. Aliyense wa iwo wachiritsidwa ndi Mphamvu ya Mulungu.”—Mkonzi]. Amen.

¹⁹⁹ (Mukuti chiyani? Chabwino... Chabwino, ayi, basi kungodutsa pamenepo. M’bale Neville ndi ine, eya, ife tiwapempherera iwo mpaka kumapeto. Chotero, sitingawabweretse iwo kuti azizungulira mbali, chifukwa inu mukhoza, ngati inu mungatero, inu muchita... Miniti chabe...?)

²⁰⁰ Tsopano ndiloleni ndiyankhule kwa gulu lodikirira: *Awa* ndi Mawu a Mulungu, Amene ine... Amene ine ndawakhalira moyo, ndipo ine ndidzawafera, mwa chisomo cha Mulungu ndi

chithandizo. Mulungu pokhala Woweruza wanga wochirimika, ine ndakuuzani inu Choonadi. Ine ndawonapo, ndipo zinthu zonse izi zikubwera kwa icho. Ngakhale kuchokera pa nsomba yaing'ono imene inawukitsidwa kumusi uko, kodi inu munayamba mwaimvapo nkhani imeneyo? Apo pakhala amuna kumbuyo kwenikweni uko, awiri a iwo, amene analipo pamenepo pamene izo zinkachitika; ndinawauziratu tsiku limodzi izo zisanachitike. Tsopano, ine ndingakuuzeni inu bwanji zinthu izi zimene ziri? Mwaona, ine ndikufuna kuti ndidzalalikire pa, umodzi wa mausiku awa, pa *Kulinganiza*. Munthu akhoza kukuuzani inu chinachake, ndi kumangopitirira kumamanga monga choncho, koma ngati palibepo Lemba kuti lilinganize izo, izo potsiriza zingagwere pansi. Ngati kuzindikira za mumtima uku, ndi masomphenya awa ndi zinthu zimene ine ndakuuzani inu, ngati izo zikanapanda kukhala Choonadi; chinthu choyamba, pali Baibulo loti liyikire izo kumbuyo, ndipo apo panali Mzimu Woyera kuti utsimikizire kuti ine ndakuuzani inu Choonadi.

²⁰¹ Tsopano, ine ndakhala pafupifupi zaka fortini pa ntchitoyi, kudutsa wotsutsa aliyense amene akanatha kupita patsogolo panga. Ophunzira, anzeru, china chirichonse, palibe nthawi imodzi iwo akanatha . . .

²⁰² Ndiye inu mukudziwa zimene iwo ananena? Inu mwazimvapo izo pano. Iwo amati, “Anthu kunja mwa osonkhana amapita kuseri, kukayankhulana ndi anthu.” Choyamba iwo anati iwo anali anthu ochokera ku tchalitchi changa, amene amapita uko kuti akachite zimenezo. Ndiye iwo samatha kuzipeza zimenezo, alipo ambiri a iwo.

²⁰³ Chinthu chotsatira iwo ananena, kuti, “Iwo amakhala abale” amene amayenda ndi ine, “iwo amaima kumbuyo uko ndi kumati, ‘Munthu *uyu* ali ndi zomvetserera, mmakutu ake.’”

²⁰⁴ Ndiye iwo ananena kuti, “Billy Paul, Billy Paul amabwera ndi—ndi kupita kumtunda uko ndi kukawerenga pa khadi, zimene anthu anena. Ngati pali chinachake chovuta ndi makutu awo, iye amati, ‘makutu awo’ kapena ‘mmimba mwawo.’”

²⁰⁵ Zimatheka bwanji mdziko iwo amene amakhala kunja uko amene amakhala opanda makadi a pemphero? Zimatheka bwanji mdziko kulosera zinthu zimene zimadzachitika mwangwiro? Izo zimatheka bwanji kuti zizichitika mwanjira imeneyo? Izo sizingatheke. Aliyense akudziwa, amene amaganiza bwino bwino.

²⁰⁶ Iwo ananena chinthu chomwe chomwecho zokhudza Yesu, pamene Filipino anapita ndikukamutenga Natanieli. “Iye anali mzake wa Yesu.” Iye anati, “Ndithudi, iye anamuuzza Yesu zonse zokhudza zimenezo. Iye akumamutsatira iye.”

207 Ndipo kenako ophunzira amenewo anati, kapena ophunzira amenewo a mpingo waukulu anati, “Munthu uyu ndi Belezebule. Iye ndi Belezebule. Iye ndi wam’bwebwe.”

208 Yesu anati, “Ine ndikukhululukirani inu chifukwa cha zimenezo. Koma tsikulina Mzimu Woyera ukadzabwera kudzachita chinthu chomwecho, mawu amodzi otsutsa Zimenezo sadzakhululukidwa.” Tsopano ngati. . .

209 Ine ndakhala woona mtima ndi anthu inu, woona mtima bas monga momwe ine ndimadziwira kukhalira. Oh, ine mwinamwake ndinatsutsanapo ndi zikhulupiriro zina, zimene inu muli nazo mu fioloje yaing’ono ndi zinthu. Koma, chifukwa chimene ine ndimachitira zimenezo, Paulo anati, “Ngati mngelo wochokera Kumwamba abwera ndi kudzalalikira chinthu china kupatula chimene Baibulo limenelo limanena,” ndi chimene iye waphunzitsa, “msiyeni iye akhale wotembereredwa.”

210 Chotero, ine ndikuyenera kungotsatira chimene Baibulo lanena. Ngati Baibulo linati, “Iye ali yemweyo dzulo ndi kwanthawizonse,” Ine ndikhulupirira zimenezo. Basi chirichonse chimene Baibulo linanena, ndizo ndendende basi zimene ine ndimakhulupirira. Ine ndimangonena izo monga chomwecho. Ine sindinakhale ndi maphunziro aliwonse, sindinakhale ndi kuphunzitsidwa kulikonse. Ine ndimangomvetsera kwa Mzimu Woyera ndi Baibulo. Ndipo kufika pano, mpaka mmawa wa Isitara uwu, kwa zaka sarte wani, Iye sanandikhumudwitsepo ine.

211 Ndipo ine ndikukuuzani inu kuti Mzimu Woyera unandiiza ine za utumiki umenewo umene ukubwera, kwa zaka ziwiri zapitazo kapena zitatu, ndipo ine ndakhala ndikuuza mipingo konsekonse. Ndipo Mulungu Wamphamvuzonse pokhala Woweruza wanga, komwe kuno mbali iyi ya Salemu, agologolo amenewo anafika pokhalapo pamene panalibe agologolo. Kumusi kumeneko ndi Charlie, ataima kumbuyo uko, ndi ambiri a iwo kumusi kuno mu Kentucky; agologolo amenewo anabwera pamalo amene iwo panalibepo, ndinanena pamene iwo akanati adzakhale. Kumene Tony ndi iwo, Banks, atakhala pamenepo. Ndipo iwo anali pamenepo, ndendende. Ndikubwerera mmbuyo, ndipo munthu woyambirira pa amene izo zinayakhulidwirapo, anali mkazi ameneyo wakhala apo, ndipo ndi zimenezo apo. Mmawa wina kumtunda kumeneko, pamene ine ndinali kudwala ndi vuto la kumero lija, ine ndinamuwona Yesu ataima patsogolo panga, ndipo Iye anandiiza ine kuti utumikiwu watsimikiziridwa kale kwa ine.

212 Tsopano chikuyenera kuchitika ndi chiyani, ine sindikudziwa. Koma, chinthu chimodzi, ine ndikuyenera kuika pambali chinacho, kuti ndikwere pa uwu. Njira yokhayo imene ine ndimaidziwa yochitira. Zidziwike tsopano, mulole izi zizokotedwe, monga Yobu ananenera mmawa uja, ndi

cholembere cha chitsulo, pa thanthwe. Ine sindikudziwa choti ndichite. Chinthu chokhacho chimene ine ndikuchidziwa, ndi kusunthira patsogolo. Iye anandiuza ine. Ndipo Mulungu ndi Woweruza wanga, Iye anandiuza ine. Ine ndakuuzani inu Choonadi. Ndipo ngati Mulungu watsimikizira ndipo ndakuuzani inu, ndipo palibe nthawi imodzi imene aliyense pano anayamba waikapo dzanja lawo pa chirichonse chimene chinali cholakwika, ndiye ichi ndi cholondola, nachonso. Icho ndi cholondola, nachonso.

²¹³ Tsopano pamene ine ndikupita apa ndikukaima kumapeto a mzere. Ine ndikhala ndi eledara, M'bale Neville pamenepo, munthu waumulungu, m'busa wathu pano, kuti aziwadzoza anthu. Ine ndiziyika manja pa anthuwo, chifukwa kutuma kwa Yesu, itatha Isitara, kunali, "Pitani mukaike manja pa odwala, iwo adzachiritsidwa."

²¹⁴ Ine sindikudziwa chimene Iye ati andiuzze ine ndikamadutsa pa mzerepo. Ine ndiyesetsa kuti ndikukhudze kudzodza kwapamwamba kumeneko. Ine sindikudziwa chimene chiti chichitike. Ine sindikudziwa. Chirichonse chimene icho chiri, ine ndingochita basi monga Iye ati andiuzire ine.

²¹⁵ Tsopano kazibwerani, kazibwerani apa ndi mtima wodzadza. Ziribe kanthu ngati Iye ati akudzuzuleni inu, ngati Iye sanena kanthu kwa inu, mosalabadira chimene icho chiri, inu muzipita mukumuthokoza Iye, inu mwaona. Chifukwa, ntchitoyo yagwirika, ndi kamtunda ndithu kuti zidzafike kwa inu.

²¹⁶ Tsopano, m'bale, ndi mwendo umenewo, ine ndikufuna kuti inu mukhulupirire izo. Ngati Iye, pa telefoni, angachotse vuto la mmimba limenero kwa inu, Iye ndithudi akhoza kuchotsa vuto la mwendo limenero kwa inu mmawa uno, mwaona. Tsopano inu mukhulupirire ndi mtima wanu wonse.

²¹⁷ Ndipo dona amene ali ndi khanda laling'ono limenelo amene anali ndi vuto la mtima, musakaikirenso. Khulupirirani! Khulupirirani!

²¹⁸ Tsopano ine ndikufuna aliyense mu tchalitchi kuti akhale mu pemphero. Ndipo ine ndikutsikira pansu kuti ndikapemphere. Nonse a inu mungokhala mu pemphero tsopano, pamene ine ndikubweretsa mzere wa pemphero uwu, kupempha, basi kumangoika manja anga pamenepo ndi kumayankhula mdalitso.

²¹⁹ Ndipo, kumbukirani, ngati aliyense wa inu ali ndi tchimo lirilonse losalapidwa, chidziwike kwa inu kuti Mulungu sadzakuchiritsani inu ndi tchimo limenero losalapa. Mulikonze ilo, inu musanabwere kudzadutsa apa, chifukwa izo zikhoza kukupangani inu kukhala moipa kwambiri. Mukuona?

²²⁰ Tsopano izo siziri mu kuzindikira za mumtima. Kuzindikira za mumtima, ine ndimazidziwa zinthu zimenezo. Koma, ndipo

uku sikuzindikira za mumtima, ine ndikufunafuna utumiki watsopano. Nonse a inu mukumvetsa bwino? Chabwino. Tsopano khulupirirani.

Tsopano tiyeni tipemphere pamene ife tikuweramitsa mitu yathu.

²²¹ Atate Mulungu, zidindo za zala zanga zidakali pa guwa ili, kwa maora ndi maora, kwa tsopano pafupifupi zaka sarte kapena kuposera, zimene ine ndakhala ndikuima pano ndikulalikirira, ndiponso kuzungulira dziko. Ndipo Inu mwatsimikizira Uthenga umene ine ndalalikirira, chifukwa Uthenga umachokera kwa Inu. Ine sindinapite ku masukulu aliwonse, sindinafunsire kwa aliyense koma Inu, kuwerenga Mawu Anu ndi kudikirira kuti ndiwone chimene Mzimu unganene kuti ndichite.

²²² Ndipo tsopano, Ambuye, Inu mukudziwa za utumiku uwu wa Marko 11:23, ndiponso podziwa kuti ora layandikirira, podziwa kuti moona ine ndanena za agologolo amenewo, ndi za Mlongo Hattie ndi anyamata ake. Tsopano, Atate, ndipo podziwa kuti masomphenya amenewo anabwera kwa ine kumtunda uko pa bedi, mmawa wina. Ine ndinaliwona Baibulo limenelo, ndipo kenako mtanda, ndipo kenako Inu. Ndipo chinaululidwa mmalingaliro anga kuti ine ndikuyenera kuvomereza izo, chifukwa izo zatsimikizidwa.

²²³ Tsopano, Ambuye, ine ndikupita chitsogolo mmawa uno mu tchalitchi changa, kuti ndidzaime apa mmawa wa Isitara uwu, ndikupemphera kuti Inu mukandidzutse ine ku mphatso yatsopano, yamphamvu kwambiri, chifukwa cha anthu, yamphamvu kwambiri. Osati chifukwa cha chipulumutso changa; chifukwa Inu munandipulumutsa ine, Ambuye, kale kale. Osati kwa inemwini; ine ndazikana kale zinthu zonse zazikulu zikulu, kuti ndikudziweni Inu. Monga Inu munanenera kwa ine kunja uko pa kachisi wamkulu uja, tsiku lina, “Ndine gawo lako.” Tsopano, Ambuye, ndiroleni ine ndikhale gawo Lanu, kuti ine ndikhoze kukonderedwa ndi Inu, kuti Mzimu Wanu udzalowe mwa ine. Ndipo pamene ine ndikuyika manja anga pa anthu ofunika awa, odwala, mulole Mzimu Wanu, Ambuye, uchite ntchito ina yonseyo. Ndizo zonse zomwe ine ndikudziwa kuzichita, Ambuye.

²²⁴ Ine ndikukumbukira kutuma kwanga, ine ndinali “unabadwa kuti udzapempherere anthu odwala, Uwapangitse iwo kuti akhulupirire, ndi kukhala owona mtima pamene iwe ukupemphera.” Ambuye, ndine basi... Ine sindikudziwa momwe ndingakhalire woona mtima mowonjezera. Ine—ine... Iwo akudwala, Ambuye. Ndipo ine—ine ndinadwalapo, inemwini. Chonde, Wokonderedwa Mulungu, perekani kuti iwo akachiritsidwe, aliyenseyo.

225 Ine ndikupita patsogolo tsopano, Ambuye, mwa chikhulupiriro, monga Mose anaponda pa Nyanja Yofiira. Ine ndikusuntha kuchoka pa guwa lopatulika ili, ndikupita pansu ku mzere wa pemphero uyu, mu Dzina la Yesu Khristu. Mulole Mulungu Amene anandipatsa ine agologolo amenewo, Mulungu Amene anapereka kwa Mlongo Hattie mawu amenewo, Mulungu Amene anapangitsa ine kuwayankhula iwo, mulole Iye apite ndi ine. Ine ndikupita mu Dzina la Yesu Khristu. [Zina za zoyankhula za M'bale Branham zikuvuta kuti uzimve pa mzere wa pemphero wotsatira—Mkonzi].

226 Satana, ine ndikutsutsa . . . iwe, mu Dzina la Yesu Khristu, kuti umusiye mwanayu. Musiye iye, tuluka mwa mwana uyu; choka, ndipo mwanayo akakhale bwino.

227 Ine ndikuika manja anga pa m'bale wanga, mu Dzina la Yesu Khristu, ndikudzudzula kusautsika kwa thupi lake. Amen.

Mu Dzina la Yesu Khristu, mupatseni iye chopempha chake.

228 Ambuye, mu Dzina la Yesu Khristu, mupatseni Mlongo Ruth machiritso ake. Amen.

229 Ine ndikumupempherera mwanayu. Koma ine—ine ndikubwera kumeneko kuchokera pa guwa ilo . . . Kodi inu mukakhala kuti? [Mlongo akuti, “Bloomington.”—Mkonzi]. Bloomington, Indiana? Mukandilembere ine kalata za mwana ameneyu. Watupa mimba yonse apa tsopano. Kodi inu mukhulupirira, dona, kuti izo ndi zoonza? [“Ine ndikukhulupirira kuti Izo nzoona.”]

230 Ndiye, Atate, ine ndikuika manja anga pa . . . mwana uyu, ndipo ndikudzudzula chiwanda ichi. Chichoke pa mwanayo. Ndipo mulole . . . ? . . . Mulole tsopano iye akhale bwino bwino ndipo mwanayo achiritsidwe.

Inu mukandilembere ine kalata, mu masiku angapo.

231 Mwaona mwana wamng'ono wa maso opingasa wagona pamenepo? Ngati inu simukaikiranso, inu mudzambweretsa mwana *ameneyo* ndi kudzamuwonetsa iye kuti ali bwino bwino ndiponso atachiritsidwa.

232 Ine ndikuika manja anga pa mlongo uyu. Ndipo mulole iye akhale ndi mawonedwe a mkazi wa Chisurofonika. Ndipo mulole iye achiritsidwe mu Dzina la Yesu Khristu . . . ? . . .

Mulole mtima ukhale bwino, mu Dzina la Yesu Khristu.

233 Ine ndikuyankhula mawu awa. Izo zikuyenera kukhala bwino. Izo sizingakhale chirichonse. Yesu anati, “Ine ndikhoza, ngati inu mungakhulupirire.” Tsopano, ngati Iye angapange agologolo kuwonekera pamenepo monga *choncho*, monga Iye anachitira ndi mwanawankhosa nthawi ina, Iye akhoza kuwupanga mtima umenewo kukhala wabwino bwino ndi wochiritsidwa. Iwo ukuyenera kutero.

Mu Dzina la Yesu Khristu, mulole mtimawo ukhale bwino. Perekani izi.

²³⁴ Tsopano, kodi zimenezo si zophweka? Izo ndi zophweka. Mulungu ndi wophweka kwambiri, ife timayenda pamwamba pa izo. Tsopano inu mungokhala ophweka kwambiri osati muziganiziranso za izo nkomwe. Izo zikhala bwino.

²³⁵ Ambuye, mulole mlongo wathu akhale bwino, mu Dzina la Yesu Khristu. Amen. Mlongo...?...

²³⁶ Ambuye, tsopano ine ndanena mawu awa, moona mtima monga ine ndingavomezere pamaso pa anthu. Ine ndawauza iwo, “Ngati inu mudzanena kwa phiri ili, ‘Suntha,’ ndipo osakaikira, inu mukhoza kukhala ndi chimene inu mwanenacho.” Mu Dzina la Yesu Khristu, mulole kusautsika uku kuchotsedwe, ndi mavuto anu onse amene inu muli nawo. Musakaikire tsopano. Mupite moyandikira chifupi ndi Iye tsopano.

²³⁷ Ambuye, ine ndikuika manja anga pa mwana uyu tsopano ndi kupweteka kwa mutu kowonjeza uku. Mu Dzina la Yesu Khristu, mulole iye achiritsidwe. Amen.

²³⁸ Ambuye, mu Dzina la Yesu Khristu, mulole phiri limenero lichoke kwa iye, mulole iye achiritsidwe. Mulole m’bale wathu tsopano akhale wamphumphu...?... Amen.

²³⁹ Wogontha ndi wosayankhula; wogontha chete. Ambuye, mu Dzina la Yesu Khristu! Ine ndaima ndi kulalikira tsiku ndi tsiku, ndi chaka ndi chaka, Ine sindinawonopo chikhulupiriro chikukhudzana ndi Inu, mmoyo wanga wonse, pokhapokhapo pamene chinachake chikuchitika! Tsopano, iye ndi wogontha mkhutu lake, ndi wovulala mmimba mwake. Mulole iye achiritsidwe, mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

Tsopano, musakaikire ayi.

²⁴⁰ Ambuye, Inu mukudziwa kusautsika kwa thupi lake. Ndi manja ataikidwa pa iye, ndi mtima woona, mulole iye achiritsidwe, mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

²⁴¹ Imfa yagona pakhomo limodzi, chikhulupiriro pa linalo. Mulungu, gudubuzani mwalawo ndipo mulole chikhulupiriro chibwerepo. Mulole khansa imusiye iye, mu Dzina la Yesu Khristu.

²⁴² Ambuye, mulole iye achiritsidwe. Ine ndikuika manja pa iye. Uthenga ukumvekabe kudzera mmakoma. Mu Dzina la Yesu Khristu, mulole kuti iye achiritsidwe.

²⁴³ Atate Mulungu, ine ndikuika manja anga pa m’bale wanga. Mulole izo zitero, Ambuye, Mzimu Wanu ndi mphamvu, kuti zimupatse iye chopempha chake. Mulole izo zitero, mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

Izo zatha. Musakaikire izo tsopano.

244 Ambuye, chokhumba cha m'bale wathu ndikubwera mu Kukhalapo Kwanu, ndi chochitika ichi pa iye. Tsopano, mu Dzina la Yesu Khristu, mulole iye akhale ndi chimene iye akuchipempha. Amen.

245 Ndi chinthu chachikulu bwanji! Mulole Mzimu Woyera ubwere pa mwana uyu, kwa ulemelero wa Mulungu kuti iwo akathe kumulera iye kwa wake...?...Chifukwa cha Ufumu wa Mulungu, mulole iye alandire izo. Amen.

246 Atate, mu Dzina la Yesu Khristu, mulole izo zikhale chomwecho, kuti mlongo wathu achiritsidwe, ndipo chopempha chake chiperekedwe, mu Dzina la Yesu. Amen.

247 Mulole izo zichitidwe. Inu mulandira Mzimu Woyera. Palibe njira yokuletserani inu ku...?...Inu mukuyenera kutero! Inu mukuyenera kulandira Iwo, chifukwa Mulungu ananena chomwecho. Inu muime ndi Iwo.

Mungodutsa pansi pang'ono pokha. Mungoti...?...

248 Atate Akumwamba, mu Dzina la Yesu Khristu, mupereke chopempha cha mlongo wathu. Amen.

249 Atate, mu Dzina la Yesu Khristu, mupereke chopempha cha mlongo wathu. Mulole iye achiritsidwe. Amen.

250 Iye akhoza kupangitsa agologolo kubwera powonekera, nthawi seveni zolunjika. Iye akhoza kumupatsa mzimayi ameneyo chirichonse chimene iye wachipempha; Iye akhoza kupereka icho kwa inu...?...

251 Ambuye, mu Dzina la Yesu Khristu, perekani chopempha cha mlongo wathu. Iwo ndi Mawu Anu. Zikomo Inu. Ndipo icho chiperekedwe kwa iye, Atate, kudzera mwa Yesu Khristu. Amen.

252 Wokonedwa anu? Atate, mu Dzina la Yesu Khristu, perekani izi...?...

253 Ambuye, mkazi wamng'ono Wachiyuda uyu...Inu ndi Mulungu wa Abrahamu. Perekani izi, mu Dzina la Yesu Khristu, chopempha chake. Izo zikhale chomwecho!

254 Mu Dzina la Yesu Khristu, Mulungu wa Kumwamba, mupereke chopempha chake. Amen.

255 Mtsikana wamng'ono uyu. Basi pamene iwe umabwera pa nsanja pamenepo, Mulungu amandiuza ine zonse za moyo wako. Iye achotsa manjenje amenewo kwa iwe.

256 Ambuye, ine ndikudzudzula manjenje mwa mtsikana uyu. Mulole iwo amusiye iye ora lino ndipo ayende akuchoka pano ali wokondwa kwambiri. Izo zichitike, mu Dzina la Yesu Khristu.

257 Mulungu wa Kumwamba, Amene munawukitsa Mwana Wanu, Yesu, mu chiwukitsiro ife tikusangalala, mulole iye asangalalire icho kwakukulu lero...?...Mu Dzina la Yesu. Amen.

258 Mu Dzina la Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu, ine ndikuika manja pa mlongo wanga, kupempha kuti iye akhoze kuchiritsidwa tsopano mu Dzina la Yesu.

259 Mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu, mulole mlongo wathu achiritsidwe. Amen. Izo sizingamusunge iye. Izo zikuyenera kuchokapo. Pitani, izi zikungoyenera kuchokapo.

260 Ambuye, mu Dzina la Yesu Khristu, mulole mlongo wathu achiritsidwe. Amen. Mu Dzina la Yesu Khristu, ine ndikumuchiritsa uyu, mlongo wanga. Amen.

Mu Dzina la Yesu Khristu, ine ndikumuchiritsa mlongo wanga. Amen.

Mu Dzina la Yesu Khristu, ine ndikumuchiritsa mlongo wanga.

Mu Dzina la Yesu Khristu, ine ndikumuchiritsa uyu, mlongo wanga.

Mu Dzina la Yesu Khristu, ine ndikumupatsa iye chopempha chake. Amen.

261 Ambuye, mu Dzina la Yesu Khristu, ine ndikumupatsa mayi wamng'ono uyu chopempha chake.

Mu Dzina la Yesu Khristu, ine ndikumupatsa iye chopempha chake, Ambuye.

Ambuye, mu Dzina la Yesu Khristu, ine ndikumupatsa iye chopempha chake.

262 Satana, ine ndikukutulutsa iwe kunja. Mu Dzina la Yesu Khristu, musiyе mkaziyu.

263 Wakhala atakumangani inu kwa nthawi yaitali. Inu mwamasuka tsopano. Inu mukhala bwino. Izo zikhala bwino tsopano, ndiye. Khulupirani izo tsopano.

264 Mulungu, mu Dzina la Yesu Khristu, ine ndikumupatsa mlongo uyu, amene ali wolumala, machiritso ake. Amen.

265 Mu Dzina la Yesu Khristu, ine ndikumupatsa mlongo uyu machiritso ake. Amen.

266 Mu Dzina la Yesu Khristu, mlongo, ine ndikukupatsa iwe machiritso ako. Amen. Izo zikhale chomwecho!

267 Ine ndikudalira kwa Mulungu kuti ine sindikulakwitsa. Perekani izi, mwa chikhulupiriro. Izi zikhale chomwecho!

268 Kodi inu mukukhulupirira Mulungu akupatsani inu mphamvu kuti zikachiritse vuto la mtima aponso? Kodi inu mukukhulupirira nkhani ija imene ine ndangoinena? Ndi mtima wanu wonse? Ndiye ine ndikukupatsani inu machiritso anu. Mu Dzina la Yesu Khristu, ine ndikukupatsani inu machiritso anu.

269 Dzina la mkazi uyu amene wangopita kumbuyo uko ndi ndani? Kodi inu mumakhala mozungulira kuno kwinakwake?

[Mlongo akuti, “Inde.”—Mkonzi]. Inu muzikumbukira kuti inu mwachiritsidwa! Izo ndi zoonza basi monga momwe ine ndaimira pano.

270 Atate mu Dzina la Yesu Khristu, perekani izi, ine ndikupempherera, machiritso ake. Amenii.

271 Atate, mu Dzina la Yesu Khristu, mulole iye alandire machiritso ake. Amenii!

272 Ine—ine—ine ndikulengeza za iwe...ine—ine—ine... Mwa chisomo cha Mulungu, kudzera mphatso Yauzimu, ine ndikukupatsa iwe machiritso ako! Kumuthamangitsa mdierekezi ameneyo, aponso.

273 Inu mukukhulupirira Mlongo Rose? O Ambuye, Mlengi wa miyamba ndi dziko lapansi, mpatseni Mlongo Rose Austin uyu machiritso awa, Ambuye, mu Dzina la Yesu Khristu. Amenii. Ndi zimenezotu, Mlongo Rose, pitani mukukhulupirira tsopano.

274 Ambuye, perekani kwa mlongo wathu machiritso ake, mu Dzina la Yesu Khristu. Amenii...?...

275 Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? Inu mukukhulupirira gawo lililonse la izo. Ndiye ine ndikukupatsani inu, mu Dzina la Yesu, chopempha chanu. Mulungu amupanga iye kukhala wabwino bwino.

276 Mulole izo zikhale chomwecho, Ambuye, kuti mchimwene wake akachiritsidwe, mwathupi ndi mwauzimu, mu Dzina la Yesu Khristu. Amenii!

Mulole ili likhale ora limene pamene...?...

277 Ambuye, ine ndikuika manja anga pa iye, pamene iye ali mwangwiro wopanda chiyembekezo, kwa madotolo kapena machiritso aliwonse ochokera ku sayansi ya zamankhwala. Koma osati pokumana ndi Khristu woukitsidwa. Mu Dzina la Yesu Khristu, mulole iye achiritsidwe. Amenii.

[M'bale Branham akuyankhula ndi mlongo—Mkonzi.]
...?...

278 Ambuye, perekani kwa mlongo wathu, mvetserani mwatcheru ku chopempha chake, kupenyenera mawu aliwonse amene iye wanena. Izo ndi chifukwa cha Ufumu. Ine ndikupemphera kuti Inu mukapereke izo kwa iye, mu Dzina la Yesu. Amenii.

[Mlongo akuyankhula ndi M'bale Branham—Mkonzi.]
...?...

279 Ambuye, monga wantchito Wanu, kumumvetsera mayi ameneyo akulirira mwana wake, ine ndikumudzudzula mdierekezi amene wachita izi.

280 Ndipo pa kuvomereza kwa chikhulupiriro cha mkaziyu, ine ndikutulutsa chiwanda ichi. Iwe sukwanitsa kumulumalitsa mwana uyu. Chiritsidwa mu Dzina la Yesu. Amenii.

Iye akungochiritsidwa kumene, mlongo. Musakaikire basi zimenezo, mpang'ono. Mulungu akudalitseni inu, m'bale. Ameneyo ndi mwana wanu? Mulole iye alandire Mzimu Woyera!

²⁸¹ Kodi inu simumutengera mwanayo penapake ndi kukamumvetsera iye maminiti ochepa chabe. Ine ndikukhulupirira kuti chinachake chachitika kwa mwanayo. Inu mulandira icho. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo?

²⁸² Mu Dzina la Yesu Khristu mulole m'bale wathu alandire machiritso ake.

²⁸³ Ambuye, mulole Mphamvu ya Mulungu wa Mphamvuzonse itsutse kusautsika kwa thupi lake, ndi kumudzadza iye ndi Mzimu Woyera. Ora lake ndi lino ndi nthawi. Mu Dzina la Yesu Khristu, ine ndikupereka Iwo kwa iye. Amen.

²⁸⁴ Shuga yapita. Inu mwalandira Mzimu Woyera. Inu mwakhala mukusautsika motalika bwanji...?...Moyo wanu wonse. Kodi inu mukukhulupirira kuti Khristu akupangani inu kukhala bwino ndipo wakuwombolani inu kukusautsika uku; wakupangani inu wabwino bwino?

²⁸⁵ Mwana wanu? Lanu—phazi lanu. Inu mwangobwera nokha? Ngati ine ndikanakhala, ngati—ngati ine ndikanakhala ndi mphamvu mkati mwa ine, mwaona! Koma ine ndikukhulupirira kuti Mulungu andithandiza ine kuti ndikhale ndi chikhulupiriro cha izo. Ine ndichita chirichonse chimene chiri mu mphamvu yanga. Kodi inu mukundikhulupirira ine? Kodi inu mukukhulupirira nkhani ija ya agologolo awo? Inu mukutero? Inu mukukhulupirira kuti izo ndi zotheka, kuti mmawa uno, kuti Mulungu akhoza kuchiritsa thupi lanu, ndipo inu muyendanso, kuyenda monga momwe mumayenera kuchitira nthawi yoyamba? Pali chinachake chimene chachitika kumene kupyolera mu mabadwidwe anu pamenepo, pali chinachake chimene chinasokoneza chinachake pang'ono ndipo inu simunakule bwino basi. Chimodzimodzi ngati mwendo kumera pamwamba pa mwendo wina, iwo umawupinimbilitsira iwo pansu. Chabwino, ngati mwendo umenewo ungachoke pa mwendo umenewo, iwo ungawongoke ndipo nkukhala bwino bwino. Mukuona? Nkulondola uko? Ilo ndi themberero. Ilo ndi themberero. Ngati themberero lingachoke, ndiye inu mukhala bwino. Mukuona?

²⁸⁶ Ambuye, ine ndikuganiza, nanga bwanji uyu akanakhala mwana wanga, nanga bwanji uyu akanakhala mchimwene wanga? Mwa chikhulupiriro, ine ndikuchotsapo themberero, mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

²⁸⁷ Ambuye, ine ndikuika manja anga pa iye ndipo ndikupempha machiritso ake, mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

²⁸⁸ Atate Mulungu, mu Dzina la Yesu Khristu, ine ndikuika manja anga pa mkazi wodwala uyu, ku machiritso ake. Amen.

Mlongo Nash, Mulungu anakupulumutsani inu kwa khansa, zaka zingapo zapitazo.

²⁸⁹ Ambuye, mupatseni Mlongo Nash chopempha chake. Monga wantchito wanu, ine ndikupempha izi. Izo zichitika. Limenero ndiro yankho, Mlongo Nash.

Mu Dzina la Yesu Khristu, mupatseni mlongo wathu chopempha chake. Amen.

²⁹⁰ [M'bale ndi mlongo akuyankhula ndi M'bale Branham—Mkonzi]. Zikomo inu, m'bale, ndipo mubwerere kwa anthu anu amene anali kumeneko. Mulole Mulungu apereke izi. Nthawi yopambana yotero, anthu anu anandizungulira pamene ine ndinali kumeneko. Inu munali ku Bombay pamene ife tinali kumeneko? Chabwino, ndiye inu mukukhulupirira zinthu izi zimene ine . . . inu mwazimva?

²⁹¹ Ambuye, pamene iye azibwerera kwa anthu ake kuwoloka nyanja, mulole iye apite atadzadzidwa ndi Mphamvu ya Mulungu, wochiritsidwa mu chopempha chirichonse chimene iye akuchipempha. Mulole iye apite ndi kukalandira icho, mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

²⁹² Mu Dzina la Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu, mulole mlongo wathu alandire chopempha chake.

²⁹³ Ambuye, mupereke chopempha cha mlongo wathu. Mulole vuto lake lithe pompano, mwa chiukitsiro kudzera mwa Yesu Khristu. Amen. Mlongo, izo zikuyenera kutero, zikungoyenera kutero basi!

²⁹⁴ [Mlongo akuyankhula ndi M'bale Branham—Mkonzi]. Inu mukufuna izi zibwerezedwe mu Uthenga? ["Inde."]

²⁹⁵ Ambuye Mulungu, pamene mkazi wachichepere uyu waima apa, osati kwa cholinga chozikonda. Iye akumupempherera mchimwene wake, ali ndi matenda mmagazi ake. Ine ndikumupatsa iye chopempha chake. Mwa utumiki woperekedwa kwa ine ndi Mngelo; ndi mwa masomphenya a Yesu Khristu, masabata pang'ono apitawo, mchipinda changa; ine ndikumupatsa mtsikana uyu chopempha chake. Amen.

²⁹⁶ Izo zikuyenera kutero. Inu mumakhala pafupi ndi kuno? [Mlongo akuti, "Memphis, Tennessee."—Mkonzi]. Memphis, Tennessee. Mudzandilembere ine kalata. Inu—inu—inu mukhala nacho chopempha chanu.

²⁹⁷ M'bale Grimsley. [M'baleyo akuyankhula ndi M'bale Branham—Mkonzi]. Mulungu akudalitseni inu, M'bale Grimsley.

²⁹⁸ Ambuye, ife tikukhoza kukumbukira utali wa kumene m'bale uyu akuchokera, ndi dzenje limene iye anafukulidwamo. Iye akufuna zochuluka za Mzimu Wanu, Ambuye. Ichi ine ndikupereka kwa iye, mu Dzina la Yesu Khristu. Kuwona ntchito zake za mmbuyo, kuti iye wayesetsa kukutsatirani Inu, ndiye,

mwa Mphamvu ya—ya utumiki unaperekedwa kwa ine ndi Yesu Khristu, wotsimikiziridwa ndi Mngelo ndi masomphenya, Ine ndikumupatsa M'bale Grimsley chokhumba chake. Mudzadzeni iye wodzaza ndi chikhulupiriro, ndipo azikhala ndi kuyenda kwa pafupi.

²⁹⁹ Bwanji ngati ine ndikanakuuzani inu, “Pitani ndipo mukakhale bwino, chifukwa cha Ufumu wa Mulungu?” Kodi inu mukukhulupirira zimene ine ndanena zokhudza agologolo amenewo ndi izo, ndipo kodi inu mukukhulupirira kuti izo ndi zoono? Ndiye, Iye, Iye amandipatsa ine choti ndiyankhule kwa ili “phiri.” . . .? . . . Inu simukhalanso ndi lina. Inu simukhalanso ndi lina. Sipakhalanso nthenda, inu nonse, muchira.

³⁰⁰ Ine ndikupereka chopempha ichi chimene iye wapempha, kwa iye, mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

³⁰¹ Atate Mulungu, perekani kwa uyu, mlongo wathu, chopempha chake, mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

Chabwino, mlongo, pitani, kakhulupirireni izo.

³⁰² Atate, pamene mkazi uyu akudutsa apa, ine ndikupemphera kuti Inu mukamupatse iye chopempha chake, mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

³⁰³ Mu Dzina la Yesu Khristu, ine ndikumupatsa mkazi uyu chopempha chake. Amen. Musakaikire izo.

³⁰⁴ [Mlongo akuyankhula ndi M'bale Branham—Mkonzi]. Inu mukukhulupirira mulandira izi? [“Inde.”] Ndiye ine ndikukupatsani inu chopempha chanu, kupyolera mu Mphamvu imene inaperekedwa kwa ine kudzera mu kutuma kwa Yesu Khristu, ndi kuchitiridwa umboni. . . ? . . . Pitani, ndipo—ndipo Mulungu akakhala nanu.

³⁰⁵ M'bale Fred, chiri pa mtima wanu ndi chiyani? [M'bale Sothmann akuyankhulana ndi M'bale Branham—Mkonzi]. M'bale Freddie Sothmann, ine ndikudzudzula chiphe chimenecho mthupi mwanu. Icho chikusiyeni inu, mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

³⁰⁶ M'bale Collins. [M'bale Collins akuyankhula ndi M'bale Branham—Mkonzi].

³⁰⁷ Ambuye, m'bale wofunika uyu akusowa ubatizo wa Mzimu Woyera. Ambuye, ndi zonse zimene ziri mwa ine, ine ndikulengeza Madalitso awa pa M'bale Collins. Perekani izi. Mulole Mzimu Woyera ubwere pa iye, ndipo mulole iye akadzadzidwe ndi Mzimu Woyera! Amen.

³⁰⁸ M'bale Collins, inu mukuyenera mulandire Iwo, Iwo ukungoyenera kuti ubwere. Mulungu amangotiyesa ife.

³⁰⁹ Ambuye, perekani chopempha chake. Mulole iye akakutumikireni Inu, ndi banja lake likakutumikireni Inu, ndi mitima yawo yonse.

³¹⁰ Mulungu, perekani kwa mlongo wathu chopempha chake. Pa zonse zimene iye wazipempha, mulole iye akalandire izo, kupyolera mwa Yesu Khristu Ambuye wathu. Amen.

³¹¹ Ambuye, mpatseni m'bale uyu mphamvu yothandizira mpingo wake. Mulole izi ziperekedwe. Ine ndikumupatsa iye mphamvu iyi, kupyolera mwa Yesu Khristu. Amen.

³¹² [Mlongo akuyankhula ndi M'bale Branham—Mkonzi]. Mlongo, ndi chinthu chowopysa chimenecho chimene inu muli nacho, manjenje. Kodi inu mukukhulupirira kuti chimene ine nditayankhule kwa inu ndi choonadi? [“Inde, ine ndikukhulupirira.”] Kodi inu mukukhulupirira zimenezo tsopano, kuti ine—ine ndinanena kwa inu choonadi? [“Inde.”] Ndiye ine ndikupereka kwa inu machiritso anu, kudzera mu Dzina la Yesu Khristu. Motsimikiza basi monga momwe ine ndaimira pa guwa, manjenje anu akusiyani inu.

³¹³ [M'bale akuyankhula ndi M'bale Branham—Mkonzi.] . . . ? . . . Izo ziri, paliponse pa inu.

³¹⁴ Ambuye Mulungu, kwa m'bale wanga wamng'ono wofunika apa, kuya ndi kuzama kwa mzimu wake kukuitana ngati chakuya kuitanira ku Chakuya. Iye akufuna Mzimu Woyera. Iye walemekeza msonkhano Wanu, Ambuye, mwanjira iliyonse imene iye akanathera. Mwa Mphamvu ya Mzimu Woyera, mulole Iwo ubwere pa m'bale wanga, ndipo iye adzazidwe ndi Mphamvu ya Mulungu ndi chisomo, Mzimu Woyera. Mulandireni iye, pamene ine ndikumupereka iye mu . . .



PITANI, MUKAWAUZE CHA60-0417M

(Go, Tell)

MAULALIKA A ISITARA

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham, woperekedwa mu Chingerezi pa Isitara Lamlungu mmawa, Epulo 17, 1960, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2021 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE

P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS

P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org